# Buku la Mphunzitsi

## Nthawiyabaibulo
## Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri

### Maphunziro C7 - C12

www.besweb.com

## Bible Educational Services

Registered Charity UK (No 1186004)

**Cholinga cha Utumiki**
Kukonzera ena maphunziro a Baibulo kuti apereke choonadi cha Yesu ku m'bado otsatira pa dziko lonse lapansi.

**Masomphenya a Utumiki**
Kupereka ku m'bado wotsatira maphunziro okwanira, m'chiyankhulo chawo powalembera ndi kuwathandiza komanso kuthandiza anzathu ena onse odzipereka pa dziko lonse.

## ZOYENERA KUDZIWA

**Zomwe a Bible Educational Services amachita**
A Bible Educational Services (BES UK) amasindikiza maphunziro a "Nthawiyabaibulo", "Moyo Watsopano" ndi "Okolola" a m'Chingerezi komanso amathandiza a Postal Bible Schools ndi mabungwe ena amene amagwiritsa ntchito maphunziro a BES ku UK ndi ku mayiko a kutsidya la nyanja pokawachezera, kugwira nawo ntchito limodzi, kuwalangiza ndi kuwaphunzitsa. BES imagwiranso ntchito pamodzi ndi magulu ena amene akugwira ntchito yomasulira maphunzirowa m'ziyankhulo zawo, pomasulira, kusindikiza ndi kupereka maphunziro kwa anthu ena. Maphunzirowa amaperekedwa mwaulere kwa ophunzira onse.

Maphunziro a Nthawiyabaibulo anayamba kugwiritsidwa ntchito ku Kumpoto kwa Ireland zake 60 zapitazo. A Bible Educational Services ndi amene ali ndi udindo woyang'anira ntchito yosindikiza maphunzirowa m'Chingerezi ndi m'ziyankhulo zina zonse. Maphunziro a Nthawiyabaibulo amasindikizidwa mu A4 ndipo amathandiza ophunzira m'madera ena kuti masabata anayi aliwonse azitha kutumiza mayankho ku Postal Bible School Centre kuti akachonge. Posachedwapa, tikuyamika a bungwe la Every Home Crusade (Bungwe la Chitsistimutso) ku Belfast, anayamba kusindikiza maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi amene amatchedwa A5. Amenewa amagwiritsidwa ntchito m'matchalichi ndi m'sukulu makamaka ku mayiko akunja kuti akhale osavuta chifukwa kumeneko njira zotumizira ndi zovuta kwambiri.

Maphunziro a BES ndi apadera kwambiri chifukwa amatha kugwiritsidwa ntchito m'nyumba kapena pa gulu (tchalichi kapena sukulu), potsatira ndondomeko imene imalola ophunzira kuphunzira kwa zaka makumi awiri. Gulu lililonse lili ndi maphunziro asanu molingana ndi zaka zawo, Amene sanayambe sukulu (Kalasi 0), zaka 5-7 (Kalasi Yoyamba), zaka 8-10 (Kalasi Yachiwiri), zaka 11-13 (Kalasi Yachitatu), zaka 14-16 (Kalasi Yachinayi). Pali ndondomeko ya kaphunzitsidwe ya zaka zitatu ya gulu lililonse molingana ndi zaka zawo. (Onani peji 4.) Magulu angathe kusintha molingana ndi kuthekera kwawo. A Bibletime Resource amapereka mpata kwa ana kuphunzira Mawu a Mulungu ndi kutha kuzindikira kufunika kwa Uthenga Wabwino pa miyoyo.

Maphunziro akupezeka m'Chingerezi pa BES website – www.besweb.com kapena kuchokera kwa Mlembi Wamkulu. Amapezekanso pa website ya ziyankhulo zina. BES ali ndi zomwe analemba zothandiza amene akufuna kugwira nawo ntchitoyi, ndipo zimenezi zilinso pa website yawo.

## Keyala

**International and Northern Ireland Secretary (stockist of all English lessons)**
Mr S Balmer, BES Office (UK), 37a Belmore Street, Enniskillen, Northern Ireland. BT74 6AA
Phone: 00 44 286 632 2462
Email: sam@besweb.com

**UK Secretary – Editorial feedback**
Mr Stephen Gillham
Email: stephen.gillham@besweb.com

**Web address:** www.besweb.com
**Email address:** info@besweb.com

## BUKU LA MPHUNZITSI

Poyamba, maphunziro awa anakonzedwa ndi cholinga choti akhale otumizira anthu, koma lero maphunzirowa akugwiritsidwa ntchito kwambiri pamene njira zotumizira ndi zosadalirika. M'madera ena monga ku mipingo ya ku Afrika, India ndi mayiko ena kulibe njira zotumizira zodalirika. Chifukwa cha ichi, Buku la Mphunzitsi linakonzedwa kuti lithandize amene sangathe kulandira pa positi. Buku la Mphunzitsi m'buku lino ndi la Kalasi 0, Yoyamba ndi Yachiwiri.

Buku la Mphunzitsi lililonse lili ndi ndime zonse zimene zili m'maphunziro a Nthawiyabaibulo. Maphunziro a Nthawiyabaibulo ndi Buku la Mphunzitsi zinakonzedwa kuti zigwire ntchito sabata lililonse. Maphunziro a mwezi wa Epulo amafotokoza za Paska ndipo a mwezi wa Disembala za Khirisimasi.

Madera ena amagwiritsa ntchito maphunziro a pa mwezi otchedwa A4, amene ali ndi maphunziro anayi ndipo ena amagwiritsa ntchito maphunziro otchedwa A5 amene ali ndi maphunziro 24. Mphunzitsi kapena mtsogoleri akuyenera kupereka maphunziro a A4, ndipo sabata lililonse azilemba mayankho a phunzirolo m'tchalichi, ku sukulu kapena ku nyumba ndi kupereka mayankhowo sabata lotsatiralo. Kumapeto kwa mwezi, mphunzitsi kapena mtsogoleri adzilandira maphunzirowo ndi kukachonga, akatsiriza abwere nawo ndi kupereka kwa ophunzirawo.

Ngati ophunzira akugwiritsa ntchito buku, mphunzitsi atenge bukulo kumapeto kwa phunziro lililonse ndi kukachonga. Koma tikudziwa kuti madera ena izi ndi zosatheka. Ngati akuphunzira m'kalasi, ophunzira asinthane mabuku awo ndipo mphunzitsi kapena mtsogoleri awathandize kupeza mayankho ndipo ophunzirawo achongelane maphunziro awo. Kumapeto kwa bukuli kuli malo oyika marikisi amene wophunzira wapeza mwezi uliwonse ndiponso malo a ndemanga ya mtsogoleri ya momwe wophunzirayo akuchitira m'kalasi. Palinso satifiketi yomwe wophunzira ayenera kulandira yoonetsa marikisi ake a maphunziro a miyezi isanu ndi umodzi.

Timakondwera pamene anthu akutifotokozera zomwe akukumana nazo pogwiritsa ntchito Buku la Mphunzitsi ndi mabuku a Nthawiyabaibulo ndipo tumizani ndemangazo kwa stephen.gillham@besweb.com.

## KUKONZEKERA KWA APHUNZITSI

Buku la Mphunzitsi si lotsekeka kuti mphunzitsi sangathenso kuyikapo zinthu zina zomwe akuziona kuti ndi zothandiza pophunzitsa. Nawa malangizo othandiza pogwiritsa ntchito Nthawiyabaibulo.

- **Kudziwa bwino nkhani** - Aphunzitsi akuyenera kudziwa bwino nkhani ya m'Baibulo komanso phunziro la Nthawiyabaibulo lomwe akugwiritsa ntchito. Nkhani ndi yakuti, mphunzitsi awerenge phunzirolo nthawi yophunzitsa isanakwane. Iye amvetse bwino ndondomeko ya phunziro lililonse kuti akonzekere bwino kuphunzitsako.
- **Kumvetsa phunziro lokaphunzitsa** - Poyamba pa ndondomeko ya phunziro lililonse pali mawu akuti, "Ife tikuphunzira kuti" motsatidwa ndi zolinga ziwiri zophunzirira zomwe mwina ana angamvetse ngati mphunzitsi atafotokoza, kenaka pali gawo lotsiriza phunziro la Nthawiyabaibulo. Cholinga chophunzirira ndi kufuna kudziwa nkhaniyo, pamene chachiwiri ndi cholimbikitsa ophunzira kuti aganizire zomwe aphunzirazo ndi kuzigwiritsa ntchito pa moyo wawo. Zolinga zimenezi zikugwirizana kwambiri ndi fundo/choonadi cha m'phunzirolo ndipo aphunzitsi akuyenera kugwiritsa ntchito zimenezi kuti adziwe momwe aphunzitsira ndi zomwe ana aphunzira.
- **Mawu oyamba** - Maphunziro onse akuyamba ndi mawu akuti, "kumene kuli ana" ali ndi zomwe akukumana nazo. Pali njira zambiri zomwe tapereka zothandiza ana kutenga mbali pa zokambirana nthawi ya maphunzirowo.
- **Kuphunzitsa** - Fundo zazikulu za phunziro tapereka. Tikuyembekezera kuti aphunzitsi sadzikhalanso akumaziwerenga pamene akuphunzitsa koma kuti akhala atadziwa bwino nkhani yonse ndipo adzitha kufotokoza nkhaniyo mochititsa chidwi. Mphunzitsi ayesetse kuti ana amvetse mitu ya maphunzirowo kuchokera pa nkhani yomwe akuphunzira ndiponso awathandize kumvetsetsa zoyenera kuchita kuchokera mu nkhaniyo. Pamene m'poyenera tayesetsa kufotokozera bwino monga nkhani chabe. Mawu amenewa tawalemba motere: ***ITALICS***.
- **Kuphunzira** - Nkhani iliyonse ili ndi Vesi Yoloweza. Malo ena muli Mavesi Oloweza awiri; taonjezera vesi ina yomwe tikuona kuti itha kukhala yothandiza kuti ana aphunzire mosavuta. Tikukhulupirira kuti ana adzaphunzira Mavesi Oloweza ndipo aziwakumbukira kotero kuti adzadziwa mavesi ambiri.

- **Kutsiriza** - Kwa amene akuphunzira m'kalasi, mphunzitsi ayenera kudziwa ngati ophunzira angathe kutsiriza ntchito yawo ndiponso za thandizo lomwe likufunika kuchokera kwa mphunzitsiyo. Kwa ophunzira ena padzafunika kuti mphunzitsi aziwerenga nkhaniyo, ophunzirawo n'kumatsatira kapena kumvera. Koma enanso adzatha kuwerenga okha nkhaniyo. M'njira zonse ziwiri, ndi kofunika kuwauza malangizo okhudzana ndi mafunso. Ngati Nthawiyabaibulo sikuchitikira m'kalasi, n'kofunika kuti aphunzitsi azipezeka kuti azithandiza kuyankha mafunso osati aziyankha ngati a m'kalasi wamba. Ophunzira ayenera kumasangalala, kulimbikitsidwa ndi kuyamikiridwa pamene kuphunzira.
- **Kukumbutsana** - Zomwe zingatheke chitani, khalani ndi nthawi ya mafunso, ya masewero ndi zina zambiri. Izi zidzathandiza kuphunzira ndi kukumbukira pamtima nkhaniyo.
- **Kuonetsa** - Nthawi zina, zinthu zoti muonetse zidzakhala zovuta kuzipeza koma ngati n'kotheka yesetsani kupeza zithunzi kapena zida zina zothandiza kuti ophunzira amvetse nkhaniyo. Zinthu zimene ophunzira akuziona zimathandiza kwambiri pofotokoza nkhani. Pamene n'zotheka, pezani zithunzi kuchokera ku www.freebibleimages.org (FBI) zomwe mungathe kulandira. Kumapeto kwa Buku la Mphunzitsi kuli zina zoonjezera momwe akufotokoza kwina kumene mungapeze zithunzi za nkhani za m'Baibulo mwaulere.
- Ngati mungapeze fotokope mutha kukulitsa zithunzizo, kukhala za kalala ndi kuzigwiritsa ntchito pophunzitsa.

## Nthawi ya Phunziro

- **Machitidwe.** M'buku la Mphunzitsi muli machitidwe a phunziro lililonse, koma mphunzitsi ali ndi ufulu nthawi ndi nthawi kusintha machitidwe ake.

  1. Mawu Oyamba ndi kufotokoza nkhani - mphindi 15
  2. Kuphunzitsa Vesi Yoloweza – mphindi 5 mpaka 10
  3. Kutsiriza kulemba - mphindi 20
  4. Mafunso ndi zochitika zina mpindi 5 mpaka 10.

Kumbukirani mawu ofunika awa:

"Ndiuzeni ndipo ndidzayiwala,
ndionetseni ndipo ndidzakumbukira,
loleni ndichite nawo ndipo ndidzamvetsetsa."

## Zophunzitsa Nthawiyabaibulo

| | KALASI 0 (sanayambe sukulu)<br>Kalasi Yoyamba (Zaka 5-7)<br>Kalasi Yachiwiri (Zaka 8-10) | Kalasi Yachitatu<br>(Zaka 11-13) | Kalasi Yachinayi<br>(Zaka 14+) |
|---|---|---|---|
| MAPHUNZIRO A | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Abrahamu<br>6. Abrahamu<br>7. Petro<br>8. Petro<br>9. Yakobo<br>10. Akhristu Oyambirira<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe<br>2. Nowa<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Pemphero<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Chilengedwe ndi Kugwa<br>2. Zochitika Zoyamba - Genesis<br>3. Petro<br>4. Petro - Mtanda<br>5. Petro<br>6. Abrahamu<br>7. Yakobo<br>8. Moyo wa Chikhristu<br>9. Paulo<br>10. Paulo<br>11. Paulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO B | 1. Moyo Woyambirira wa Khristu<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Mafanizo<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yosefe<br>7. Yosefe<br>8. Alembi a Uthenga Wabwino<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Mose<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Mafanizo<br>2. Zodabwitsa<br>3. Betaniya<br>4. Ambuye Yesu - Mtanda<br>5. Akhristu Oyambirira<br>6. Yakobo ndi Banja Lake<br>7. Yosefe<br>8. Machitidwe 2:42 - Zoyenera Kuchita<br>9. Mose<br>10. Mose<br>11. Lamulo<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |
| MAPHUNZIRO C | 1. Danieli<br>2. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>3. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute ndi Samueli<br>6. Davide<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Yona<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Anthu Amene Yesu Anakumana Nawo<br>3. Zodabwitsa Zina Zambiri<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Amene Mulungu Anawagwiritsa Ntchito - Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi | 1. Danieli<br>2. Zoyankhula za Yesu<br>3. Mphamvu za Ambuye<br>4. Imfa ya Khristu<br>5. Rute<br>6. Samueli<br>7. Davide<br>8. Yoswa<br>9. Eliya<br>10. Elisa<br>11. Anthu Ena a mu Chipangano Chakale<br>12. Nkhani ya Khrisimasi |

<u>C7 Nkhani Yoyamba</u>

**Davide akuthawa – Iyi ndi nkhani ya bwenzi la pamtima la Davide.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Jonatani anaonetsa kuti anali bwenzi labwino pothandiza Davide.<br>● Ambuye Yesu angathe kukhala Bwenzi lathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Samueli 20: 17***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 20: 1-42*** |
| **MAWU OYAMBA** | Ana a Kalasi 2 akhale awiriawiri kwa mphindi imodzi kapena ziwiri akukambirana za khalidwe la bwenzi labwino. Kenaka afotokozere gulu lonse yankho lawo. Ngati n'kotheka, lembani mayankho pa bolodi. Tsindikani za makhalidwe amene bwenzi likuyenera kuonetsa pamene mnzake ali pa mavuto. Chitsanzo, bwenzi amathandiza, kuteteza ndipo amakhala nawe nthawi zonse. Perekani zitsanzo zinthu zochitika molingana ndi gulu.<br>Njira ina, ana a Kalasi 1 akhale ndi thumba m'mene muli zinthu zodzitetezera monga chipewa, mafuta oteteza ku dzuwa, mankhwala otsukira mano ndi mswachi, magolovesi, chithunzi cha lamba wa m'galimoto ndi zina zambiri. Sankhani mwana woti asankhe chinthu ndi kufotokoza momwe zimatetezera. Fotokozani kuti Mulungu amatipatsa anthu amene amatiteteza – makolo, akuluakulu ena (tchulani mayina), abwenzi. Mu nkhani ya lero, tiphunzira za momwe bwenzi labwino linatetezera Davide. |
| **PHUNZITSANI** | ● *Onaninso moyo wa Davide mu C6 pofunsa mafunso ofunika awa: Kodi chikonzero cha Mulungu pa moyo wa Davide chinali chotani? Kodi mfumu anali ndani pamene Davide anawuzidwa kuti adzakhala mfumu? Uzani ana kuti Sauli ankachitira Davide nsanje. Afunsani apeze chifukwa chake. Zifukwa zina zitha kukhala kupha Goliati, kupambana pa nkhondo, ndi Mulungu kukhala mbali yake. Kumbutsani ana zomwe anachita Sauli pofuna kuonetsa nsanje yake (C6 Nkhani Yachinayi). (Kwa Kalasi 2 mutha kufotokoza momwe nsanje imakhudzira ana ndi zomwe Baibulo likunena za nsanje.)*<br>● *Kumbutsani ana za mwana wa Sauli, Jonatani, amene anali bwenzi lenileni la Davide. Fotokozaninso makhalidwe a Jonatani amene munalemba m'gawo la "Mawu Oyamba".*<br>● Mfumu Sauli anali ndi phando lalikulu lomwe linatha masiku angapo. Davide ankayenera kukhala nawo koma anaganiza kuti sakhala nawo. Jonatani anali wokonzeka kuthandiza Davide pofufuza ngati Sauli ankaganiza zochitira zoyipa Davide. Iye anakonza zokumana ndi Davide mseri m'munda nthawi ina. Kumeneko adzagwiritsa ntchito chizindikiro kuti Davide adziwe ngati ndi wotetezedwa kapena ali pa chiopsezo. ***(1 Samueli 20: 4-23)*** *Fotokozani kuti Mulungu ankasamalira Davide pomupatsa bwenzi lapadera kuti limuteteze.*<br>● Sauli anazindikira tsiku lachiwiri la phwando kuti Davide panalibe. *Fotokozani zomwe iye anachita.* ***(1 Samueli 20: 27-34)*** *Kodi mukuganiza kuti Jonatani anamva bwanji mu mtima mwake? Ganizirani zomwe tsopano Jonatani adzachita. Kodi adzakhala wokhulupirika kwa Davide ndi kumufotokozera choonadi chonse?*<br>● *Phunziro la Nthawiyabaibulo lilibe gawo lofotokoza momwe mivi inagwirira ntchito ngati chizindikiro kwa Davide za chiopsezo chake. Inu mutha kuonjezera zimenezi kuti nkhani imveke bwino.* M'mawa otsatira Jonatani anapita m'munda m'mene Davide anabisala kuseri kwa mwala. Iye anapita ndi mnyamata wamng'ono. Mnyamata anaponya mivi itatu patsogolo pa Davide. Davide anadziwa kale kuti chizindikiro ichi chinkasonyeza kuti moyo wake unali pa chiopsezo ndi kuti ankayenera kuthawa. ***(1 Samueli 20: 35-40)***<br>● Jonatani atawuza mnyamata amene anali ndi mivi ija kuti abwerere ku mudzi, inali nthawi yabwino yoti Davide ndi Jonatani ayankhulane. *Kambiranani zomwe Davide ankamva mu mtima mwake pokhala ndi bwenzi monga Jonatani.* Kunali kovuta kutsanzikana koma analonjezana kuti adzakhala abwenzi nthawi zonse. ***(1 Samueli 20: 41-42)***<br>● Yankhulani za kuti Ambuye Yesu ndi Bwenzi lathu tikamuyitana m'miyoyo yathu kukhala Mpulumutsi. Kambiranani muyeso wa chikondi chake pamene anatifera ndi kukhulupirika kwa chikondi chake tsiku ndi tsiku zomwe zimaonekera potithandiza ndi kutiteteza. Lumikizani makhalidwe a bwenzi amene ali mu gawo la "Mawu Oyamba".<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI mu Zoonjezera A – Davide ndi Jonatani / Davide akuthawa. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Samueli 20: 17.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Ngati muli ndi chilichonse chimene ana amakonda kuseweretsa mutha kufanizira ndi mnyamata uja amene anali ndi mivi. Gwiritsani ntchito mafunso awiri awa m'magulu awiri:<br>- Kodi Sauli ankayembekezera kuti Davide akhala kuti?<br>- Kodi Jonatani ndi Davide anakumana kuti?<br>- Kodi ndi liti limene Sauli anazindikira kuti Davide palibe?<br>- Kodi iwo analonjezana chiyani?<br>- Kodi Sauli anachita chiyani za Davide?<br>- Kodi mukuyenera kuchita chiyani kuti Yesu akhale bwenzi lanu lenileni? |

## C7 Nkhani Yachiwiri

**Davide amusiya Sauli wosamupha – Iyi ndi nkhani ya Davide kukhululukira Sauli.**

**Ife tikuphunzira kuti:**

- Davide sanayesere zobwezera choyipa pa Sauli.
- Mulungu akufuna kuti tizichita zisankho zoyenera za momwe tikukhalira ndi anthu ena.

**Vesi Yoloweza:** ***Aefeso 4: 32***
**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 24: 1-22***

### MAWU OYAMBA

Kambiranani nthawi zimene ana amakumana ndi wina amene anawachitira zoyipa. Kodi iwo amachita chiyani? Kodi iwo amafuna atabwezera zoyipa munthuyo? Yesani kugwiritsa zitsanzo zenizeni zimene zikukhudzana ndi ana. Fotokozani kuti ngati Ambuye Yesu ndi Mpulumutsi wathu, Iye adzatithandiza kusankha zoyenera kuchita ndi kukhululukira ena.
Mu nkhani yathu lero, tiphunzira momwe Davide anachitira kwa Mfumu Sauli.

### PHUNZITSANI

*Onaninso zomwe Sauli anamuchitira Davide mu nkhani zathu zam'mbuyo (C6 Nkhani Yachinayi ndi C7 Nkhani Yoyamba).*

- *Fotokozani za chipululu kumene Davide ankabisala. Yankhulani za mapanga ndi kukula kwake komanso mdima wake!* Pamodzi ndi anthu 3000, Sauli anapita kukafunafuna Davide. Ndipo Sauli analowa m'phanga lina m'mene Davide anabisalamo pamodzi ndi anthu ake. *Khalani chete – kodi Sauli amupezadi Davide?* Sauli sanazindikire kuti Davide anali pafupi kwambiri m'phanga lomwelo. ***(1 Samueli 24: 1–3)***
- Anthu a Davide anaona kuti uyu unali mpata woti athane ndi Sauli ndipo anakakamiza Davide kuti amuphe. *Thandiza ana kuti aganizire mwayi umene Davide anali nawo. Kodi zikanakhala zabwino kuti Davide aphe Sauli? Fotokozani kuti nthawi imeneyi Sauli anali mfumu yodzodzedwa ndi Mulungu ngakhale ankachita zoyipa zambiri. Kumbutsani ana kuti Mulungu analonjeza kuti Davide adzakhala mfumu. Kodi chilipo kapena alipo amene akanasintha lonjezo limeneli? Mulungu anakhala akuteteza Davide mpaka nthawi imeneyi – pamene ankapha Goliati komanso pamene Sauli ankafuna kumupha ndi mkondo. Tsindikani kuti moyo wa Davide unali m'manja a Mulungu ndipo palibe amene akanasintha malonjezo ndi chikonzero cha Mulungu pa moyo wake. Davide ankayenera kudzakhala mfumu pa nthawi ya Mulungu.* ***(2 Samueli 2: 1–4)***
- Davide ankadziwa kuti sizinali zabwino kuti iye aphe Sauli. *Fotokozani momwe iye anayendera kukafika pamene panali chofunda cha Sauli ndi kudula msonga yake!* Davide anadikira mpaka pamene Sauli anatuluka m'phangamo. ***(1 Samueli 24: 4–7)***
- Kenaka Davide anayenda ndi kukayima pa khomo la phangalo ndi kuyitana Sauli mofuwula. *Ganizani za kudabwa kwa Sauli!* Davide anaonetsa Sauli msonga ya chofunda chake chimene anadula. *Kodi Sauli ankayenera kuzindikira chiyani pamenepo?* Davide anafotokozera Sauli kuti anasiya wosamupha. Sauli anakhudzika mu mtima. Iye anazindikira kuti Davide wakhala ali wabwino kwa iye ndipo sanamuchitire zomuyenera. Nthawi imeneyi, Sauli anasiya kuthamangitsa Davide komanso kufuna kumupha. ***(1 Samueli 24: 22)***
- *Zimene anachita Davide kwa Sauli ndi chithunzithunzi cha zimene Mulungu amachita kwa ife. Iye anatichitira chifundo ndi kutikhululukira ngakhale ndife osayenera kukhululukidwa. Iye anapereka njira yoti ife tikhululukidwe kudzera mu imfa ya Ambuye Yesu. Pamene takhulupirira Yesu ndi machimo athu akhululukidwa, ife nthawi zonse tikuyenera kutsatira chitsanzo chake ndi kukhala okonzeka kukhululukira ena.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Davide mfumu / Davide amusiya Sauli wosamupha.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'kofunika Vesi Yoloweza - ***Aefeso 4: 32***. Vesi iyi yagawika yokha magawo atatu, choncho ana athe kutsatira ndi kuchita sewero m'magulu atatu.

### KUMBUKIRANI

Ana a Kalasi 2 akhale m'magulu kuti achite sewero la kukhululukira ena (onani "Mawu Oyamba"). Ana a Kalasi 1 achekenire zilembo zikuluzikulu za mawu ofunika a mu nkhani ya lero – chifundo, chabwino, kukhululuka. Iwo amate zimenezi pa pepala ndi kuyika pa khoma kuti aziona ndi kukumbukira nkhani ya lero.

## C7 Nkhani Yachitatu

**Davide akhala Mfumu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kusunga malonjezo ake.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Mulungu anasunga malonjezo ake kwa Davide a kukhala mfumu.<br>● Mulungu analonjeza Davide kuti kudzakhala Mfumu yayikulu kuposa iye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Agalatiya 2:20 kapena 2 Samueli 5: 4***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Samueli 31: 1-13, 2 Samueli 5: 1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za kuti nafe timakhala ndi nthawi yayitali yodikira zomwe ena anatilonjeza. Perekani zitsanzo zoyenerana ndi msinkhu wa ana. Davide naye anali ndi nthawi yodikira pa moyo wake. Bwerezani zimene ana akudziwa kale za iye powafunsa mafunso ndipo inu mufotokozere bwino pamene n'koyenera kutero. Kodi Davide anachokera m'banja laufumu (i.e. Kodi abambo ake anali mfumu)? (Ayi, Davide sanala mwana wa mfumu. Iye anachokera m'banja la anthu wamba.) Kodi iye ankagwira ntchito yanji? (m'busa wa ziweto) Kodi ndi ndani amene anasankha iye kukhala mfumu? (Mulungu - iye anadzodzedwa ndi mneneri Samueli.) Tsindikani kuti Davide anali chisankho cha Mulungu, ndipo kuti Mulungu adzakwaniritsa chikonzero chake chomukhazikitsa monga mfumu ngakhale nthawiyo panali mfumu ina. Kodi anali ndani? Sauli anabweretsa mavuto pa Davide, koma Davide anapitiriza kudalira Mulungu. |
| **PHUNZITSANI** | ● Tsiku lina Sauli ndi banja lake anaphedwa pa nkhondo. Davide anamva chisoni kwambiri chifukwa cha Sauli, ngakhale ankazunza Davideyo, ndi mwana wake Jonatani amene anali bwenzi lenileni la Davide. ***(1 Samueli 31: 1–6)*** Davide analemba ndakatulo yapadera yokumbukira Jonatani. ***(2 Samueli 1: 17-27)***<br>● Mosakhalitsa anthu anabwera kwa Davide. *Chifukwa chiyani?* Iwo anakumbutsa Davide za kuti iye adzasamalira anthu a Israyeli pokhala mtsogoleri wawo. *Lumikizani mawu awa ndi moyo wa Davide poyamba ngati m'busa wa ziweto.* Lonjezo la Mulungu tsopano likukwaniritsidwa! Davide anali ndi zaka makumi atatu pamene anakhala mfumu. Iye analamulira zaka makumi anayi! ***(2 Samueli 5: 1-5)***<br>● Kenaka Davide anatenganso mzinda wa Yerusalemu umene unali m'manja mwa adani a Mulungu. Kumeneko, Davide anamanga nyumba yaufumu yokongola. Ife tikuwuzidwa kuti mphamvu za Davide zinapitirira kukula chifukwa Yehova Mulungu Wamphamvuzonse anali naye. *Phunzitsani ana kuti ifenso tikuyenera kukhala ndi Mulungu.* ***(2 Samueli 5: 9–11)***<br>● Davide anali wokonzeka kumanga Nyumba ya Mulungu kuti azikapembedza Mulungu. *Fotokozani kuti mpaka nthawi imene ankapembedza Mulungu mu tenti yotchedwa Chihema.* Koma mmodzi mwa aneneri, Natani, anapereka uthenga kwa Davide wa kuti sichinali chikonzero cha Mulungu pa Davide. Kudzera mwa Natani, Mulungu anakumbutsa Davide zinthu zonse zabwino zimene Iye anamuchitira ndipo analonjezanso chinthu china chopambana cha kuti mmodzi m'banja la Davide adzakhala mfumu yamuyaya. *Funsani ana kuti aganizire kuti ameneyu ndi ndani. (Fotokozani nkhani ya mwana amene anabadwira mu Betelehemu kapena mfumu imene anzeru a kum'mawa ankayifunafuna.) Thandizani ana kuti amvetse za kuti Davide ankafuna kutamanda Mulungu.* ***(2 Samueli 7)*** *Mutha kuwerenga mawu a Davide mu nyimbo ya matamando, mwachitsanzo pa* ***vesi 22****.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Davide atamanda Mulungu / Davide akhala mfumu. |
| **PHUNZIRANI** | Vesi Yoloweza ***2 Samueli 5: 4*** ndi mawu onena zoonadi za Davide monga mfumu. ***Agalatiya 2: 20***, amene akupezeka mu Kalasi 1 ndi 2 mu Nthawiyabaibulo, akufotokoza mwachidule za zomwe Ambuye Yesu anatichitira ndipo ndi mawu ofunika kuti tiwaloweze. |
| **KUMBUKIRANI** | Ana a Kalasi 1 achekenire akolona.<br>Mafunso a "Ndani" akubwereza nkhani ya Davide pomwe yafika:<br>● Ndani analonjeza Davide kuti adzakhala mfumu?<br>● Ndani anadzodza Davide ku nyumba ya abambo ake?<br>● Ndi ndani amene Davide anapha ndi legeni?<br>● Ndani ankafuna kupha Davide ndi mkondo?<br>● Ndani anali bwenzi lenileni la Davide?<br>● Ndani anabisala m'phanga?<br>● Ndani anaphedwa pa nkhondo?<br>● Ndi ndani amene Davide anamutamanda? |

## C7 Nkhani Yachinayi

**Davide ndi Mefiboseti – Iyi ndi nkhani ya Davide kuonetsa kukoma mtima.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Davide anasunga malonjezo ake kwa bwenzi lake Jonatani poonetsa kukoma mtima kwa Mefiboseti.<br>● Mulungu amaonetsa kukoma mtima kwa ife.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Samueli 9: 7***<br>**Ndime Yowerenga:** ***2 Samueli 9: 1-13*** |
| **MAWU OYAMBA** | Gwiritsani ntchito zitsanzo zoyenerana ndi ana kuti athe kuganizira msanga za kukomera mtima ena, monga: wina amene wagwa pansi, wayiwala kanthu kena, ali ndi zambiri zoti anyamule, ali ndi ntchito zambiri zoti agwire, alibe wosewera naye…? Pa sukulu mutha kufunsa ana kuti apereke zitsanzo zawo kapena mutha kufotokoza za ana ena amene anaonetsa kukoma mtima. Mu nkhani ya lero, Davide ankafuna kuonetsa kukoma mtima kwa munthu wina. Fotokozani kuti kukhala ndi mtima ofuna kuonetsa kukoma mtima kwa anthu ena ndi chinthu chabwino! |
| **PHUNZITSANI** | ● *Kumbutsani ana Nkhani Yachitatu pamene tinaphunzira momwe Mulungu anakwaniritsira malonjezo ake kwa Davide.* Tsopano Davide ndi mfumu ndipo m'dziko muli mtendere. Koma Davide sanayiwale bwenzi lake labwino Jonatani ndiponso malonjezo amene anachita kwa wina ndi mnzake. *Fotokozani kuti ndi chinthu chabwino kukwaniritsa malonjezo amene munachita kwa ena.* Davide anafuna kudziwa ngati analipo wina wa m'banja la Jonatani amene anali ndi moyo kuti amukomere mtima. Iye anafunsa Ziba amene anali wantchito wa Mfumu Sauli ngati ankadziwa wina aliyense. ***(2 Samueli 9: 1-3)***<br>● Ziba nthawi yomweyo anakumbukira Mefiboseti. *Fotokozani zinthu zomvetsa chisoni zomwe zinachitika kwa Mefiboseti ndi za kuvulala kwake. Kodi Mefiboseti mmene ankakula ankamva bwanji mu mtima mwake? Samalani zoyankhula zanu ngati m'gulu lanu muli ana amene akukumana ndi zovuta ndipo limbikitsani gulu lanu kuyamika Mulungu chifukwa cha zinthu zabwino zimene ali nazo pa moyo wawo.*<br>● Mefiboseti nthawi imeneyi ankakhala kutali kwambiri ndi Yerusalemu ndipo sankatha kuyenda. *Lingalirani zomwe iye anaganiza atalandira uthenga omuyitana kuti apite ku nyumba yaufumu.* ***(2 Samueli 9: 3-5)*** *Mwina iye anachita mantha?*<br>● Mfumu Davide anafotokozera Mefiboseti kuti sankayenera kuchita mantha. Koma ankafuna kumuchitira zabwino. Iye ankafuna kuonetsa kukoma mtima chifukwa cha Jonatani komanso chifukwa cha ubwenzi umene unali pakati pa Davide ndi Jonatani. Davide anaonetsa kufewa manja pa zimene anapereka kwa Mefiboseti. *Mutha kulemba mphatso ndi ufulu wake, kapena kujambula zithunzi zofotokoza mphatso iliyonse:*<br>*1) malo amene anali a Mfumu Sauli*<br>*2) antchito ochuluka olima m'minda yake*<br>*3) malo okhala ndi kudya pa tebulo la mfumu*<br>● *Fotokozani kuti kudya ndi mfumu zinkatanthauza kuti iye anali ngati mmodzi wa m'banja la mfumu.* Mefiboseti modzichepetsa analandira zomwe Davide anamupatsa, kuzindikira ukulu wake ndi kukoma mtima kwa Davide. ***(2 Samueli 9: 6-13)***<br>● *Nkhani iyi ikutiphunzitsa kumvetsetsa za kukoma mtima kwa Mulungu pa ife. Machimo athu amatilekanitsa ndi Mulungu, koma Mulungu ndi wokonzeka kutilandira m'banja lake. Ife si oyenera chikondi chotere, koma Mulungu amachititsa kuti zitheke kudzera mwa Mwana wake Ambuye Yesu amene anatifera pa mtanda. Limbikitsani ana kuti alandire kukoma mtima kwa Mulungu pa kumuyamika chifukwa cha Ambuye Yesu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Davide ndi Mefiboseti. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani Vesi Yoloweza imene ndi mbali ya Ndime Yowerenga ya lero, kapena phunzitsani ***Tito 3: 4***: "Koma pamene kukoma mtima, ndi chikondi cha pa anthu, cha Mpulumutsi wathu Mulungu zinanoneka,..anatipulumutsa ife." |
| **KUMBUKIRANI** | Ana a Kalasi 2 akhale m'magulu kuti apange posita imene ikuonetsa njira zomwe Mulungu amaonetsera kukoma mtima kwake kwa ife. Ana a Kalasi 1 akhale ndi nthawi ya mafunso. Mulembe mafunso kuseri kwa zithunzi zomwe zamatidwa pa tebulo ya mfumu ndi mawu osiyanasiyana pa fundo iliyonse.<br>● Ndi ndani amene anali Mfumu yokoma mtima?<br>● Ndi ndani amene anali bwenzi lapadera la Davide?<br>● Ndani anawuza Davide za Mefiboseti?<br>● Chinachitika ndi chiyani kwa Mefiboseti pamene anali wamng'ono?<br>● Ndi zinthu ziwiri ziti zomwe Davide anapereka kwa Mefiboseti?<br>● Kodi Mefiboseti ankayenera kumadya kuti kuyambira nthawi imeneyi?<br>● Ndi ndani amene waonetsa kukoma mtima kwa ife?<br>● Pezani mawu amene akusowa: "Koma pamene kukoma mtima, ndi chikondi cha pa anthu, cha Mpulumutsi wathu ________ zinanoneka,..anatipulumutsa ife." |

## C8 Nkhani Yoyamba

**Yoswa akhala mtsogoleri watsopano – Iyi ndi nkhani ya kudziwa kuti Mulungu ali ndi anthu ake.**

**Ife tikuphunzira kuti:**
- Mulungu analonjeza kukhala ndi Yoswa ndi kumuthandiza.
- Mulungu amatithandiza pa ntchito yomwe amatipatsa kuti tigwire.

**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 1: 9***
**Ndime Yowerenga:** ***Yoswa 1: 1-18***

### MAWU OYAMBA

Kalasi 2 – Funsani ana za amene akulamulira pa sukulu yawo kapena dera lawo. Kodi chimachitika ndi chiyani munthuyo akachoka? Kodi amalowa m'malo mwake ndani, ndipo tsopano wolamulira ndi ndani? (mwina wachiwiri wake) Yankhulani za kufunika kokhala ndi wina wolamulira, kuti iwo azichita ziganizo ndi kukhala ndi udindo woyang'anira onse amene ali pansi pawo. Kukhala wolamulira ndi kupanga malamulo zimaoneka ngati zabwino ndi zosangalatsa, koma fotokozani za udindo wawo pa ntchitopo. Nkhani ya lero ndi ya munthu watsopano amene akuyamba kulamulira.
Kalasi 1 – Kambiranani ndi ana momwe iwo ankamvere mu mtima ngati atasankhidwa kuti achite chinthu china chatsopano ndi chovuta. Mu nkhani ya lero Yoswa akuyamba ntchito yatsopano.

### PHUNZITSANI

- Mulungu anayankhula kwa Yoswa ndi kumuwuza kuti Mose wamwalira ndipo tsopano iye ndiye adzatsogolere anthu kulowa m'Dziko la Malonjezano. ***(Yoswa 1: 1-2)*** *Kodi Yoswa anamva bwanji mu mtima mwake?*
- Anthu ankayenera kukonzekera kuwoloka Mtsinje wa Yordano ndipo Mulungu anakonzeka kuwapatsa dziko limene analonjeza zaka zambiri m'mbuyomo. Aisrayeli anafika malo amenewa zaka makumi anayi m'mbuyomo koma anachimwa ndipo sanakhulupirire Mulungu, motero iwo anakhala akuyendayenda mu chipululu. ***(Yoswa 1: 3)*** *Kambiranani zomwe Aisrayeli ankamva mu mtima mwawo. (kusangalala, kukondwa, kudabwa, mantha)*
- *Werengani mawu amene Mulungu anayankhula kwa Yoswa m'mavesiwa. Onetsani ana momwe Mulungu akuyankhulira mobwereza malangizo ake akuti iye akhale wamphamvu ndi wolimba mtima. Kodi izi zikanathandiza Yoswa motani monga mtsogoleri watsopano? Fotokozani kuti iye akanatha kukhala wotere osati chifukwa cha mphamvu zake kapena maluso ake koma chifukwa Mulungu analonjeza kuti adzakhala naye.* ***(Yoswa 1: 5-7, 9, 18)***
- Mulungu anakumbutsanso Yoswa za lamulo ndi zolamulira zimene Mulungu anapereka kwa Mose. Yoswa ankayenera kuphunzira ndi kumvera. Ngati iye adzasunga malamulo a Mulungu, Mulungu adzadalitsa anthu m'nyumba zawo zatsopano. ***(Yoswa 1: 7-8)*** *Fotokozani kufunikanso kwa ife kumvera Mulungu.*
- Kenaka Yoswa anawuza anthu onse ayike pamodzi katundu wawo ndi kukonzekera kuchoka. Anthu analonjeza Yoswa kuti monga iwo anamvera ndi kutsatira Mose, iwo adzamveranso ndi kutsatira Yoswa. ***(Yoswa 1: 10-11, 16-18)*** *Pamene takhulupirira Ambuye Yesu ndi kumulola kulowa m'miyoyo yathu, Iyenso amalonjeza kukhala nafe ndi kuti sadzatisiya.*

**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**
**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yoswa akhala mtsogoleri watsopano.

### PHUNZIRANI

Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yoswa 1: 9.***

### KUMBUKIRANI

Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi:
- Kodi ndani anamwalira?
- Kodi dzina la mtsinje umene ankayenera kuwoloka ndi chiyani?
- Kodi Mulungu anati Yoswa ankayenera kukhala wotani?
- Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa Yoswa?
- Kodi Yoswa ankayenera kuwerenga ndi kuphunzira chiyani?
- Kodi anthu anagwirizana kuchita chiyani?

## C8 Nkhani Yachiwiri

## Yoswa ndi dziko latsopano – Iyi ndi nkhani ya chikhulupiriro cha Rahabi mwa Mulungu.

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Rahabi anakhulupirira ukulu wa Mulungu wa Israyeli.<br>● Mulungu akufuna kuti tikhale ndi chikhulupiriro mwa Iye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 2: 24***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yoswa 2: 1-24*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana ngati akudziwa za kukazonda. Kodi kufunika kwa mzondi ndi kotani? Kodi chimachitika ndi chiyani mzondi akagwidwa? Kodi chingachitike ndi chiyani mutapezeka mukuthandiza mzondi amene akuthandiza adani anu? |
| **PHUNZITSANI** | ● Anthu awiri analowa m'Dziko la Malonjezano mu mzinda waukulu wa Yeriko. Iwo ankayenera kukazonda ndi cholinga choti Israyeli adziwe momwe angagonjetsere dzikolo. Mzinda wa Yeriko unazunguliridwa ndi makoma akuluakulu amene anali ndi zipata. Makoma ake anali aakulu mulifupi ndipo anamanga nyumba pamwamba pake. Mayi wina wotchedwa Rahabi ankakhala m'nyumba imodzi pa khomalo.<br>● Anthu awiriwa anali m'nyumba ya Rahabi. Mwatsoka anthu ena anaona azondiwa ndipo anakawuza mfumu ya Yeriko. ***(Yoswa 2: 1-2)*** *Funsani ana aganize zomwe zichitike tsopano.*<br>● Mfumu inatuma amithenga ku nyumba ya Rahabi kuti atenge anthuwo, koma Rahabi anawabisa pa denga la nyumba yake ndi kuwaphimba ndi udzu. Iye anauza amithenga a mfumu kuti anachedwa kufika chifukwa anthuwa anali atachoka kale. Kenaka asilikali a mfumu anatuluka kukafuna azondiwo kunja kwa mzinda. ***(Yoswa 2: 3-7)***<br>● Nthawi imeneyi Rahabi anawuza azondi aja kuti dziko lonse linkachita mantha chifukwa cha Aisrayeli. Iwo anamva zimene Mulungu anachita komanso kudziwa kuti Mulungu adzawaononga. Rahabi anapempha azondiwo ngati akanapulumutsa iye pamodzi ndi abale ake. ***(Yoswa 2: 8-13)*** *Fotokozani kuti izi zinkaonetsa kuti Rahabi ankakhulupirira ukulu ndi mphamvu ya Mulungu ndi kuti anali wokonzeka kudalira Mulungu ameneyu kuti amupulumutse. Iye anali asanapeze mpata wodziwa Mulungu monga Aisrayeli koma anali wokonzeka kumukhulupirira. Kukhala ndi chikhulupiriro zikutanthauza kudalira Mulungu. Mulungu amakondwera pamene tikukhulupirira Iye.*<br>● Azondi analonjeza kumuteteza Rahabi ngati iye sawuza anthu ena kuti iwo anali kumeneko. Iwo anamuwuza kuti adzamange chingwe chofiira pa zenera la nyumba yake ndipo amene adzakhala m'nyumbamo adzapulumuka. Kenaka azondi aja anatsika pa chingwe ndi kuthawa. (Fotokozani kuti nyumba ya Rahabi inali ndi zenera loyang'ana kunja kwa mzindawo.) ***(Yoswa 2: 14- 21)*** *Kalasi 2 - Fotokozani kuti mu Chipangano Chatsopano muli chaputala chimene akufotokoza za anthu ambiri chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Werengani* ***Ahebri 11: 31****.*<br>● Anthu aja atafika kwa Yoswa anafotokoza zimene anamva ndi kuti Mulungu anali mbali yawo ndiponso aliyense ankawaopa. Ulendo wawo okazonda unawathandiza kumvetsa za ukulu wa Mulungu. ***(Yoswa 2: 23-24)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yoswa ndi dziko latsopano. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yoswa 2: 24.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa monga njira yobwereza nkhaniyi:<br>● Kodi Yoswa anatuma azondi angati?<br>● Kodi azondi analowa m'nyumba ya ndani?<br>● Kodi Rahabi anawabisa kuti azondiwo?<br>● Kodi iye anafunsa azondiwo kuti achite chiyani?<br>● Kodi azondiwo anathawa motani?<br>● Kodi iwo anawuza Yoswa chiyani? |

## C8 Nkhani Yachitatu

**Yoswa ndi Mtsinje wa Yordano – Iyi ndi nkhani ya mphamvu ya Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Palibe chinthu chomukanika Mulungu.<br>● Ife tikuyenera kumvera Mulungu pa chilichonse chimene akutiwuza.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yoswa 3: 5***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yoswa 3: 1-17; 4: 1-24*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana za chinthu china chimene anawawuza kuti achite ndipo iwo ankaganiza kuti chinali chosatheka. Mwina ntchito yolemba ku nyumba kapena ntchito ina ya sukulu yomwe ankaganiza kuti inali yovuta kugwira. Kodi iwo anathetsa bwanji vuto limenelo? Kodi panali wina amene anawathandiza? Yoswa ankayenera kutenga Aisrayeli onse ndi kupita nawo tsidya lina la Mtsinje wa Yordano. Unali mtsinje waukulu ndipo panalibe milatho kapena mabwato. Kodi mukuganiza kuti ndi ndani amene akanawathandiza? |
| **PHUNZITSANI** | ● Yoswa ndi anthu onse ananyamula katundu wawo ndipo anayenda kupita ku Yeriko. Iwo anayima m'mbali mwa Mtsinje wa Yordano ndi kumanga misasa yawo. ***(Yoswa 3: 1)*** *Funsani ana kuti aganizire zomwe anthuwo ankalingalira.*<br>● Patatha masiku atatu, Yoswa anatumiza uthenga m'misasa yonse kuti aliyense akonzekera kuyenda. Iwo ankayenera kutsatira ansembe amene ananyamula Bokosi la Chipangano. (Ili linali Bokosi lopatulika limene linkawakumbutsa kuti Mulungu anali pakati pawo.) Yoswa anawuza anthu kuti akonzekera za tsiku lotsatira; Yehova adzawachitira zinthu zodabwitsa. ***(Yoswa 3: 2-5)***<br>● Yoswa anawuza ansembe kuti akhale patsogolo pa anthu onse ndipo ayende ndi kulowa mu Mtsinje wa Yordano. Ansembe anachita zomwe Yoswa ananena ndipo mapazi awo atangoponda m'mbali mwa madzi, mtsinje unaleka kuyenda, madzi anaunjikana, ndipo ansembe anayima powuma. (Mutha kuwawuza kuti nthaka inali youma osati ya matope, ngakhale kuti poyamba panali madzi.) ***(Yoswa 3: 6-16)*** *Kambiranani zomwe anthu anachita pamenepa.*<br>● Kenaka anthu onse anawoloka mtsinje powuma ndipo anakamanga misasa yawo mbali inayo ya mtsinje kufupi ndi Yeriko. ***(Yoswa 3: 17)***<br>● Anatenga miyala khumi ndi iwiri mu mtsinje wa Yordano ndi kuyika mbali ina ya mtsinjewo monga chikumbutso cha m'tsogolo cha zimene Mulungu anachita tsiku limeneli. *Ndi zabwino kwa ife kumakumbukira nthawi zimene Mulungu anatithandiza.* Iwo atachita zonse, Yoswa analamula ansembe kuti achoke mu mtsinje. Mapazi a ansembe atangoponda powuma, mtsinje unayambanso kuyenda monga kale. ***(Yoswa 4: 1-9)***<br>● Anthu anazindikira kuti Mulungu anali ndi Yoswa monga mmene analili ndi Mose. ***(Yoswa 4: 14)*** *Pamene takhulupirira Ambuye ndi kumvera Mawu ake m'miyoyo yathu, nthawi zonse Iye adzatithandiza.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yoswa ndi Mtsinje wa Yordano. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani Vesi Yoloweza yomwe ndi mbali imodzi ya nkhaniyi: ***Yoswa 3: 5***. |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi anthu anawoloka mtsinje uti?<br>● Kodi ndi ndani anayamba kulowa mu mtsinje?<br>● Kodi iwo anali atanyamula chiyani?<br>● Kodi madzi anachita chiyani?<br>● Kodi ndi anthu angati amene anatha kuwoloka?<br>● Kodi iwo anatenga chiyani mu mtsinje?<br>● Kodi miyalayo inali ya chiyani?<br>● Kodi iwo anazindikira chiyani za Yoswa? |

# C8 Nkhani Yachinayi

## Yoswa ndi Yeriko – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kupereka chipambano.

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Yoswa anatsatira malangizo a Mulungu kuti agonjetse Yeriko.<br>● Ife tikuyenera kukhulupirira ndi kumvera Mulungu pa chilichonse chimene angatiwuze kuti tichite.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Ahebri 11:30***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yoswa 6: 1-25*** |
| **MAWU OYAMBA** | Tiyerekezi kuti inu muli ndi ntchito yovuta kwambiri kuti mugwire. Kodi zingakhale zothandiza:<br>● Ngati mutapatsidwa malangizo ndi munthu wodalirika?<br>● Ngati munthuyu atalonjeza kugwira nanu ntchitoyo?<br>Izi ndi zimene zinachitika pa nthawi imene Aisrayeli amagonjetsa Yeriko. |
| **PHUNZITSANI** | ● *Thandizani ana kuti akumbukire momwe unalili mzinda wa Yeriko. Kodi ndi ndani ankakhala m'menemo? (Nkhani Yachiwiri)*<br>● Mulungu anawuza Yoswa kuti Yeriko anali wokonzeka kuti athire nkhondo koma sinkaoneka choncho ayi. Anthu anali ataseka zipata zonse ndipo palibe ankaloledwa kulowa kapena kutuluka mu mzindamo. Iwo ankaona kuti anali otetezedwa chifukwa cha khoma lalikulu lomwe linazungulira mzindawo. ***(Yoswa 6: 1)***<br>● Kenaka Yoswa anapereka malangizo kwa anthu amene analandira kwa Mulungu. Iwo ankayenera kuyenda kuzungulira mzindawo kamodzi pa tsiku kwa masiku asanu ndi limodzi. Patsogolo pakhala asilikali, pambuyo pake ansembe asanu ndi awiri atanyamula malipenga a nyanga za nkhosa, kutsatana ndi ansembe amene ananyamula Bokosi la Chipangano, pambuyo penipeni asilikali. Anthu ankayenera kumayenda mwakachetechete koma akuyimba malipenga. ***(Yoswa 6: 2-11)*** *Kodi Yoswa anali ndi chifukwa chochitira mantha? Tsindikana kuti kutsatira chikonzero cha Mulungu kumabweretsa chipambano. Yoswa anali ndi lonjezo la kupezeka kwa Mulungu pakati pawo (Nkhani Yoyamba) ndipo ankadalira mphamvu ya Mulungu ndi kukhulupirika kwake. (Nkhani Yachitatu)*<br>● Tsiku lililonse anthu ankadzuka m'mawa ndi kuyenda kuzungulira mzinda kamodzi. (Izi zinkatenga nthawi yayitali ndithu - unali mzinda waukulu. Komanso fotokozani kuti mwina anthu a mu Yeriko ankayima pamwamba pa khoma kuona kudzera m'mazenera zachilendo zomwe zinkachitikazo. Tsiku lililonse, anthu ankabwera kudzaona zachilendozi anthu oyenda mwakachetechete.) ***(Yoswa 6: 12-14)***<br>● Tsiku lachisanu ndi chiwiri linafika. *Fotokozani nkhaniyi mopatsa chidwi pofuna kuonetsa chiyembekezo chimene anthu ankayendawo anali nacho atayenda kasanu ndi kawiri tsiku limeneli.* Ansembe atayimba malipenga, Yoswa analamula anthu kuti afuwule. Pamene anthu ankafuwula makoma a Yeriko anagwa ndipo asilikali anathamanga kulowamo ndi kupha anthu onse anthu atafuwula. ***(Yoswa 6: 15-21)***<br>● Yoswa analamula azondi aja kuti apite ku nyumba ya Rahabi kukamutulutsa pamodzi ndi abale ake onse mu mzindamo. Iye pamodzi ndi abale ake onse anapulumuka ndipo ankakhala pakati pa Aisrayeli kuyambira nthawi imeneyo mpaka m'tsogolo. ***(Yoswa 6: 22- 23)***<br>● Yoswa analamula asilikali kuti asatenge ndi kusunga golide kapena siliva kapena zinthu zina zilizonse zofunika, komwa abwere nazo ku Nyumba ya Mulungu kuti akazipatulire kwa Iye. Asilikali ndi anthuwo ankadziwa kuti si iwo amene anagonjetsa adani, koma Mulungu. Mzinda unaononongedwa ndi kutenthedwa mpaka pansi. ***(Yoswa 6: 24-25)***<br>● *Motero Mulungu anathandiza Yoswa ndi Aisrayeli kugonjetsa mzinda woyipa wa Yeriko. Pamene tadalira Mulungu, Iye adzatithandiza kugonjetsa zoyipa zonse m'miyoyo yathu.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera A – Yoswa ndi Yeriko. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Ahebri 11: 30.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyi:<br>● Kodi Yoswa ndi ankhondo ake anadziwa bwanji zoyenera kuchita?<br>● Kodi anthu a mu Yeriko anali kuti pamene ankhondo ankafika?<br>● Kodi ankanyamula chiyani pozungulira mzinda?<br>● Kodi ansembe ankayimba chiyani?<br>● Kodi anthu ankazungulira kangati mzinda tsiku lililonse?<br>● Kodi zimenezi anachita masiku angati?<br>● Kodi tsiku lachisani ndi chiwiri anachita chiyani?<br>● Kodi chinagwetsa makoma ndi chiyani?<br>● Kodi ndi ndani anapulumutsidwa?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani ndi mzinda wa Yeriko? |

<u>**C9 Nkhani Yoyamba**</u>

**Eliya amvera Mulungu – Iyi ndi nkhani ya kumvetsera ndi kuchita zimene Mulungu akunena.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Eliya anamvera Mulungu pamene anawuza Mfumu Ahabu uthenga wa Mulungu.<br>● Ife tikuyenera kumvera chimene Mulungu akunena m'Baibulo.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 5***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Mafumu 17: 1-7*** |
| **MAWU OYAMBA** | Uzani ana kuti alembe zosowa zawo ndi zofuna zawo ndipo asiyanitse pakati pa ziwirizi. Kapena funsani munthu wina kuti abisale kapena kubisa chinthu kuti ana achifunefune ndi kuchipeza. Fotokozani kuti munthu mu nkhani iyi anapita kukabisala. |
| **PHUNZITSANI** | ● Mfumu Ahabu sankakonda Mulungu ndipo inali mfumu yoyipitsitsa imene inakhalapo mu Israyeli (onani ***1 Mafumu 16: 30***). Iye ankapembedza milungu imene sinali yoona komanso yopangidwa ndi anthu. Iye anakwatira mkazi woyipa kwambiri, Mfumukazi Yezebeli. *Kodi Mulungu ankamva bwanji ndi zimenezi?* Mulungu anakwiya kwambiri chifukwa cha zoyipa zonse m'dzikomo ndipo anafuna kulanga Ahabu. Mulungu anasankha Eliya, munthu amene ankakonda Mulungu, kuti akhale mthenga wake. Iye anapita kukawuza Ahabu kuti simudzagwa mvula kapena mame mu dziko la Israyeli kwa nthawi yayitali. *Werengani mawu a Eliya kwa Ahabu.* ***(1 Mafumu 17: 1)*** Eliya anamvera Mulungu ndipo anawuza Mfumu Ahabu nkhani yoyipayi.<br>● *Kodi mukuganiza kuti mfumu inamva bwanji mu mtima mwake ndi nkhani imeneyi? Inapsa mtima. Kambiranani zomwe zikanachitika – mbewu ndi ndiwo za masamba sizikanakula, ziweto ndi anthu akanakhala opanda madzi akumwa ndi zakudya.* Mfumu Ahabu anakwiya kwambiri chifukwa cha uthenga wa Eliya ndipo inkafuna kumupha! Koma Mulungu anali ndi chikonzero china chofuna kuteteza Eliya. Iye anawuza Eliya kuti akabisale! Eliya ankayenera kupita pa ulendo nthawi yotentha, kutsikira ku chigwa cha Keriti. Kumeneko kunali mtsinje ndipo Eliya ankayenera kumwa madzi ake. Mulungu anadzamupatsanso chakudya mu njira yodabwitsa kwambiri. M'mawa uliwonse ndi madzulo, akhwangwala adzabweretsa buledi ndi nyama. ***(1 Mafumu 17: 2-4)*** Mulungu ankasamalira Eliya. Eliya anamvera Mulungu ndipo ananyamuka kupita ku chigwa cha Keriti.<br>● Tsiku ndi tsiku Mulungu ankamupatsa Eliya zosowa zake. Eliya ankamwa madzi ochokera mu mtsinje ndipo akhwangwala ankabweretsera chakudya. Pa kupita kwa nthawi, Eliya anaona kuti mtsinje uja madzi akuwuma. *Funsani ana afotokoze ngati akudziwa chifukwa chake.* Kunalibe mvula monga Mulungu ananenera. Madzi anayamba kuchepa ndipo tsiku lina onse anatha. Kodi tsopano Eliya akanachita chiyani? Mulungu anali kale ndi chikonzero china pa Eliya! Chimene ankayenera kuchita ndi kumvera basi. ***(1 Mafumu 17: 5-7)***<br>● *Eliya anamvera Mulungu ngakhale ankadziwa kuti kuwuza Ahabu nkhani yoyipa kunali kuopsa kwambiri kwa iye. Iye anamveranso Mulungu ndipo anapita ku Keriti kumene Mulungu ankamuputsa chakudya ndi madzi. Eliya analimba mtima kuchita zomwe Mulungu anamuwuza kuti achite ndipo iye anadalira Mulungu kuti adzamusamalira.*<br>● *Mulungu amayankhula nafe lero kudzera m'Baibulo. Iye amatiwuza momwe tingakhalire komanso kukhala mmodzi mwa ana ake. Ife tikuyenera kumvetsera zimene Mulungu akunena m'Baibulo ndi kumvera. Iye amayang'anira ndi kusamalira amene amakonda Iye.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyababaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Eliya amvera Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Mafumu 17: 5****. Sankhani gawo loyamba pa vesiyi kwa ana aang'ono.* |
| **KUMBUKIRANI** | Jambulani chithunzi cha chinthu chimodzi kuchokera pa m'ndandanda umene tatchula mu gawo la "Mawu Oyamba" aja. Chitsanzo: chakudya, madzi, mthunzi, chokwera ndi zina. Iwo atha kuzionetsera polemba mawu akuti "Mulungu amakwaniritsa zosowa zathu" - kapena MAFUNSO:<br>● Kodi mayina a mfumu yoyipa ndi mkazi wake anali ndani?<br>● Kodi Mulungu ankafuna kuchita chiyani polanga Mfumu Ahabu?<br>● Mulungu anasankha ndani kukawuza mfumu chikonzero cha Mulungu?<br>● Kodi Ahabu anayankha motani?<br>● Kodi Mulungu anatumiza Eliya kuti?<br>● Kodi Mulungu anasamalira motani Eliya kumeneko?<br>● Kodi kenaka chinachitika ndi chiyani ndi mtsinjewo?<br>● Kodi tikuphunzira chiyani za Eliya mu nkhaniyi?<br>● Kodi tingamvere Mulungu motani? |

**C9 Nkhani Yachiwiri**

**Eliya adalira Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kusamalira Eliya.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Eliya ndi mayi wamasiye anakhulupirira Mulungu kuti adzakwaniritsa zosowa zawo.<br>● Mulungu wapereka njira yokwaniritsira za kusowa chathu cha moyo wosatha.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 17: 14***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Mafumu 17: 8-24*** |
| **MAWU OYAMBA** | Gwiritsani ntchito zithunzi za sabata yatha ndipo mulole ana abwereze nkhani yonse. Onetsa ufa ochepa uli mu chitini ndi mafuta mu botolo. Kodi ndingapange chiyani? Onetsani lofu ya buledi. Kodi buledi amapanga motani? (kolezani moto) Onetsa nkhuni. Fotokozani kuti ufa ndi mafuta atha kupanga buledi ochepa kwambiri. Zinthu zimenezi zili mu nkhani yathu ya lero. |
| **PHUNZITSANI** | ● Mulungu anawuza Eliya kuti achoke ku Keriti ndi kupita ku mudzi wotchedwa Zarefati. *Fotokozani zomwe Mulungu anawuza Eliya – kuti mayi wamasiye adzamupatsa chakudya. Uzani ana kuti afotokoze kuti mayi wamasiye ndi ndani.* Eliya anamvera ndipo ananyamuka ulendo wautali. Iye anakhulupirira kuti Mulungu adzamusamalira. Pamene anafika pa chipata cha mudziwo, iye anaona mayi atawerama akutola nkhuni zomwe zinagwa mu mtengo. *Fotokozani zomwe anakambirana pa vesi 10-12. N'chifukwa chiyani mayi wamasiye ndi mwana wake analibe chakudya chokwanira?* Kunalibe mvula ndipo mbewu zopangira ufa sizinamere. Anthu adzafa ndi njala. ***(1 Mafumu 17: 8-12)***<br>● *Fotokozani zomwe Eliya ananena kwa mayiyo ndi zomwe Mulungu analonjeza* ***(vesi 13-14).*** *Kodi mukuganiza kuti mayiyo anachita chiyani?* Mayiyo anadalira ndi kukhulupirira kuti Mulungu adzakwaniritsa lonjezo lake. Iye anapita ndi kuphika buledi wa Eliya ndipo kenaka anaphika wake ndi mwana wake. China chake chodabwitsa chinachitika! Pamene anayang'ana mu mtsuko wa ufa, anaona kuti unalipobe ndipo m'botolo munali mafuta. Ufa ndi mafuta zinkayenera kutha akatengamo. Koma tsiku ndi tsiku mu mtsuko munali ufa ndipo m'botolo munali mafuta; sizinathe. Zinachitika monga mmene Mulungu ananenera! Panali chakudya cha tsiku lililonse cha Eliya, mayiyo ndi mwana wake. Mulungu anasunga lonjezo lake. Iye anakwaniritsa zosowa zawo. ***(1 Mafumu 17: 13-16)***<br>● *Gawo lomaliza la Ndime Yowerenga* ***(1 Mafumu 17: 17-24)*** *zatchulidwa mu Kalasi 2 Nthawiyabaibulo.* Mwachisoni, tsiku lina mwanayo anadwala kwambiri ndipo anamwalira. Iye ananyamula mwanayo ndi kupita naye kwa Eliya. Eliya anamunyamula kupita naye ku chipinda chake ndi kumugoneka pa bedi lake. Eliya anapemphera katatu: "Inu Yehova Mulungu wanga, bwezeretsani moyo wa mwanayu." Mulungu anamva pemphero la Eliya ndipo mwanayo anayamba kupuma! Iye anamunyamula ndi kukamupereka kwa mayi wake. Mulungu anaonetsatu mphamvu yake ndi ubwino wake kwa mayi wamasiye, mwana wake ndi kwa Eliya! Mulungu sanakwaniritse chakudya cha tsiku ndi tsiku kokha, koma anaukitsanso mwana wa mayi wamasiyeyu. Mayi anazindikira kuti Mulungu wa Eliya ndi Mulungu woona.<br>● *Mulungu leronso amakwaniritsa zosowa zathu – chakudya, mabanja ndi abwenzi. Koma ife tikusowanso chinthu china chofunika kwambiri. Ife tikufuna Mulungu kuti atikhululukire tchimo lathu – zolakwa zimene timachita. Mulungu anatumiza Mwana wake, Yesu, kudzafa kuti machimo athu akhululukidwe. Ngati titapempha, Mulungu adzatikhululukira tchimo lathu. Kambiranani tanthauzo la zimenezi.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Eliya adalira Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Mafumu 17: 14***. Fotokozani kuti Mulungu amakwaniritsa lonjezo lake. Iye amakwaniritsa malonjezo ake onse m'Baibulo. |
| **KUMBUKIRANI** | M'magulu a atatuatatu chitani sewero la pa ***1 Mafumu 17: 10-16***.<br>● Kodi Mulungu anawuza Eliya apite kuti pamene madzi mu mtsinje wa Keriti anaphwa?<br>● Kodi kumeneko anakaona ndani?<br>● Kodi mayiyo ankachita chiyani?<br>● Kodi iye anapempha chiyani?<br>● Kodi yankho la mayiyo linali lotani?<br>● Kodi lonjezo la Mulungu kwa mayiyo linali lotani?<br>● Kodi Mulungu anakwaniritsa motani lonjezo lake?<br>Mafunso a KALASI 2<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani kwa mwana wa mayi wamasiyeyo?<br>● Kodi Eliya anapemphera kangati?<br>● Kodi ndi mphamvu ya ndani imene inamuukitsa?<br>● Kodi chimene ife tikusowa kwambiri ndi chiyani? |

## <u>C9 Nkhani Yachitatu</u>

**Eliya atumikira Mulungu – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kupereka chipambano kwa Eliya.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Mulungu anapereka chipambano kwa Eliya pa mpikisano wa pa Phiri la Karimeli.<br>● Mulungu wa m'Baibulo ndi Mulungu woona.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Mafumu 18: 39***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Mafumu 18: 1-2, 16-46*** |
| **MAWU OYAMBA** | Fotokozani kuti mpikisano ndi chiyani pogwiritsa ntchito zitsanzo monga masewero a mpira pakati pa matimu awiri. Yankhulani zisankho za tsiku ndi tsiku – mitundu yabwino, chakudya, nyimbo. Anthu a mu nkhani yathu akufunsidwa kuti achite chisankho chofunika kwambiri. |
| **PHUNZITSANI** | ● Mvula sinabwere kwa zaka zitatu mu Israyeli. *Fotokozani zomwe zikutanthauza – popanda mbewu, udzu, ndiwo za masamba, ndipo nyama ndi anthu kufa. Kumbutsani ana chifukwa chomwe Mulungu ankalangira Israyeli m'njira imeneyi – kuyipa kwa Mfumu Ahabu ndi kupembedza milungu ya bodza.* Mulungu anawuza Eliya kuti apite kwa Mfumu Ahabu ndi kumamuwuza kuti posachedwa Mulungu adzatumiza mvula. Eliya anamvera. ***(1 Mafumu 18: 1-2)***<br>● Mfumu Ahabu anali wokwiya ndi Eliya. *Kodi iye anaopseza kuti amuchita chiyani? (kumupha)* Nthawi iyi iye anati Eliya ndiye woyambitsa mavuto. *Fotokozani yankho la Eliya pa* ***vesi 18****.* Inali nthawi yoti aonetse kuti Mulungu weniweni ndi uti. Eliya anayitanitsa mpikisano pa Phiri la Karimeli moyang'anana ndi nyanja. *Fotokozani zomwe zinachitika pa* ***vesi 19 ndi 20*** *komanso zomwe Eliya anawuza anthu pa* ***vesi 21****.* ***(1 Mafumu 18: 16-21)***<br>● Mpikisano unali pakati pa mulungu wabodza Baala ndi Mulungu weniweni. Fotokozani za kumangidwa kwa maguwa awiri ansembe ndi nsembe zimene anayikepo. *Iwo amene ankakhulupirira Baala ndi Eliya amene ankakhulupirira Mulungu woona ankayenera kupemphera kuti moto utsike ndi kutentha nsembe zawo pa guwa. Pa guwa pamene pagwe moto, zidzaonetsa kuti Mulungu wawo ndi woona.* ***(1 Mafumu 18: 22-26)***<br>● Anayamba kupemphera anali aneneri a Baala. Iwo anapemphera kummawa konse, koma mulungu wawo sanayankhe, moto sunabwere. Iwo anafuwula kwambiri, koma palibe amene anawayankha. *Funsani ana ngati akudziwa chifukwa chake.* Iwo ankapemphera kwa milungu yopangidwa ndi miyala imene sinkamva. ***(vesi 25-29)*** Tsopano inali nthawi ya Eliya. Pamene anayika nsembe pa guwa, Eliya anathirapo migolo yamadzi khumi ndi iwiri. *Chifukwa chiyani? Kuti zikhale zovuta kuti moto uyake.* Eliya anapemphera kwa Mulungu wa Israyeli. *Fotokozani pemphero lake pa vesi* ***36 ndi 37****.* Nthawi yomweyo moto ochokera kwa Mulungu unatsika ndi kupsereza nsembe ndi miyala ya guwa ndi kuumitsa madzi wonse. Mulungu wamoyo anamva pemphero la Eliya ndipo anaonetsa mphamvu yake yayikulu. Anthu ataona zimene zinachitika, anagwa pansi ndi kufuwula: "Yehova, Iye ndi Mulungu." ***(vesi 38-39)*** Eliya analamula kuti aneneri a Baala aphedwe. ***(vesi 40)***<br>● Ichi chinali chipambano cha Eliya ndi Mulungu wake! *Kodi Eliya analonjeza Ahabu chiyani koyambirira kwa nkhaniyi?* Monga momwe analonjezera Mulungu, mlengalenga munada ndi mitambo, mphepo inawomba ndipo mvula yamphamvu inagwa. ***(1 Mafumu 18: 41-46)***<br>● Anthu a Israyeli anaona tsiku limeneli kuti Mulungu ndi Mulungu yekhayo woona. *Kumbutsani ana zomwe Eliya anayankhula pa* ***vesi 21****.* Iwo anasiya kupembedza milungu yabodza ndipo anayamba kupembedza Mulungu woona. *Anthu ambiri lero amapembedza milungu yabodza. Mulungu wa m'Baibulo ndi Mulungu woona. Kodi ndinu okonzekera kulola kuti Mulungu woona akhale woyamba m'miyoyo yanu ndi kulandira Mwana wake, Yesu, kukhala Mpulumutsi ndi Ambuye?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Eliya apemphera kwa Mulungu / Eliya atumikira Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Mafumu 18: 39.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti abwereze nkhani pogwiritsa ntchito zithunzi kapena kuyankha mafunso.<br>● Kodi Eliya anapereka uthenga wotani wochokera kwa Mulungu kwa Mfumu Ahabu?<br>● Kodi Mfumu Ahabu inati Eliya ndi ndani?<br>● Kodi yankho la Eliya linali lotani?<br>● Kodi anthu anapatsidwa chisankho chotani? ***(vesi 21)***<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani pamene anthu okhulupirira Baala anapemphera?<br>● Kodi Eliya anachita chiyani kuti kukhala kovuta kuti moto utenthe nsembe?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani Eliya atapemphera?<br>● Kodi anthu anachita ndi kunena chiyani?<br>● Kodi ndi lonjezo lina liti lomwe Mulungu anakwaniritsa kumapeto kwa nkhaniyi? |

## C9 Nkhani Yachinayi

**Eliya akhumudwitsa Mulungu – Iyi ndi nkhani ya munthu wamantha kuyiwala Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Pamene Eliya anali ndi mantha, anayiwala kudalira Mulungu kuti adzamusamalira.<br>● Ife titha kudalira Mulungu nthawi zonse.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Salimo 62: 8***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Mafumu 19: 1-16*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani zomwe Mulungu anachita kuthandiza Eliya mu nkhani zathu:<br>1) Kumupatsa malo abwino kuti abisale<br>2) Kumuteteza kwa Mfumu Ahabu<br>3) Kumupatsa chakudya<br>4) Kuonetsa mphamvu yake kwa opembedza Baala<br>Kodi mukuganiza kuti sikanakhala zosavuta kuti Eliya adalire Mulungu kuyambira tsopano? |
| **PHUNZITSANI** | ● Mkazi wa Mfumu Ahabu, Yezebeli woyipa, anakwiya kwambiri pamene anamva zomwe zinachitika pa Phiri la Karimeli ndi kuti Eliya anapha aneneri a Baala. *Bwerezani nkhani ya pa Phiri la Karimeli ngati mulibe m'Mawu Oyamba.* Kodi anthu a Israyeli anali ataphunzira chiyani? Mulungu wa Eliya anali Mulungu woona. Mwa mkwiyo, Yezebeli anatumiza uthenga kwa Eliya onena kuti adzamupha tsiku limenelo chifukwa cha zomwe anachita. Eliya atamva izi, anachita mantha ndipo anathawa kupulumutsa moyo wake! Iye anadziona ngati anali yekha ndi wachisoni ndipo anayiwala kudalira Mulungu. *Yankhulani kwa ana za nthawi zimene amaona ngati ali okha komanso achisoni pamene kusekedwa ndi anzawo ku sukulu kapena kukangana.* Mulungu amadziwa zonse zimene zimatichitikira ndi zimene zimatichitsa mantha ndi kutimvetsa chisoni. ***(1 Mafumu 19: 3)***<br>● Eliya anathamanga nthawi yotentha kupita ku chipululu kwa fumbi ndi kukhala pansi pa mtengo. Iye anapempha Mulungu kuti amulole kuti afe ndipo kenaka anagona tulo. *Uzani ana za chakudya chomwe mngelo anabweretsa.* Mulungu amasamalira amene amamukonda. Atadya ndi kugona, Eliya anali ndi mphamvu ndipo anayenda usana makumi anayi ndi usiku makumi anayi mpaka ku Phiri la Horebu (Phiri la Sinai). *Funsani ana ngati akukumbukira zimene zinachitika kumeneko – Mulungu anapatsa Mose malamulo khumi. Eliya anakhala m'phanga usiku umenewo.* ***(1 Mafumu 19: 3-9)***<br>● *Fotokozani funso limene Mulungu anafunsa Eliya ndi yankho lake.* Eliya anafotokozera Mulungu mmene ankamvera mu mtima mwake ndi chifukwa chimene anali wachisoni. Mulungu amamvetsera nthawi zonse. Mutha kumuwuza zomwe mukumva mu mtima mwanu ndipo chifukwa chomwe muli ndi chisoni komanso mantha. *Bweretsani Vesi Yoloweza -* ***Salimo 62: 8. (1 Mafumu 19: 9-10)***<br>● Mulungu anawuza Eliya kuti apite ndi kukayima pa phiri. Mulungu adzakumana ndi Eliya pamenepo. Kunabwera mphepo yamphamvu, chivomerezi ndi moto koma Mulungu sanayankhule ndi Eliya mu zimenezi. Kenaka Eliya anamva mawu onong'ona. Anali Mulungu amene ankayankhula. Iye anawuza Eliya kuti abwerere kumene wachokera. *Fotokozani zimene Mulungu ananena ndi ntchito yatsopano ya Eliya. Mulungu anali wokonzeka kugwiritsa ntchito Eliya monga mthandizi wake ngakhale ankachita mantha ndiponso kuyiwala kudalira Iye.* Ntchito imodzi anamupatsa inali yokapeza mnyamata wotchedwa Elisa amene adzakhala mneneri wa Mulungu kapena mthenga. Eliya anali atakalamba ndipo moyo wake unali uli kumapeto. Iye anatumikira Mulungu bwino. ***(1 Mafumu 19: 11-16)***<br>● *Mulungu ankayankhula ndi Eliya pa moyo wake wonse ndi kumuwuza zoti achite. Mulungu amayankhulanso lero kudzera mu zimene timawerenga m'Baibulo. Ngati muli ndi chisoni kapena mantha, pemphani Mulungu kuti akhale nanu ndi kukuthandizani. Mutha kudalira Mulungu nthawi zonse.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Eliya apempheranso / Eliya ayiwala Mulungu / Eliya akhumudwitsa Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Salimo 62: 8***. Mulungu sasintha. Iye nthawi zonse amakhala pafupi ndi ife. |
| **KUMBUKIRANI** | Ana ajambule kapena kulemba m'ndandanda wa zochitika mu nkhani kapena kuyankha mafunso:<br>● Kodi ndi ndani anaopseza Eliya?<br>● Kodi Eliya anachita chiyani ataopsezedwa?<br>● Kodi iye anapempha Mulungu kuti amulole kuti atani?<br>● Kodi mngelo anamupatsa chakudya chiti?<br>● Kodi Eliya anayenda masiku angati kuti akafike ku Phiri la Horebu?<br>● Kodi Mulungu anafunsa funso lanji, nanga Eliya anayankha chiyani?<br>● Tchulani zinthu zitatu zimene sanali Mulungu amene ankayankhula kwa Eliya?<br>● Kodi anamuputsa ntchito yotani kuti agwire?<br>● Kodi inu mumayankhula ndi Mulungu pamene muli ndi chisoni kapena mantha? |

## C10 Nkhani Yoyamba

**Elisa – Kuyitanidwa kutsatira - Iyi ndi nkhani ya Mulungu kukhala nafe.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Mulungu anapereka mphamvu kwa Elisa yogwirira ntchito yake.<br>● Mulungu adzathandiza amene amakonda ndi kutumikira Iye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 2: 14***<br>**Ndime Yowerenga:** ***1 Mafumu 19: 19-21, 2 Mafumu 2: 1-15*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani ntchito zimene anthu amagwirira ntchito ya Mulungu – amishoni, kugwira ntchito m'tchalichi, m'mabungwe a Chikhristu, kulalikira ena za Yesu.<br>*Yankhulani ndi ana za zinthu zimene amaziona kuti ndi zovuta kuchita – zolemba za ku sukulu, kusunga ndalama zawo, kulephera kusakwiya, ndi zina.* Nthawi zina timafuna thandizo kuchokera kwa anthu ena. Munthu amene ali mu nkhani yathu ankafuna thandizo la Mulungu kuti agwire ntchito imene anamupatsa. |
| **PHUNZITSANI** | ● Kodi Mulungu anasankha ndani kuti alowe m'malo mwa Eliya kukhala mtumwi yake yatsopano? *Onaninso malangizo a Mulungu kwa Eliya pa* ***1 Mafumu 19: 15-16.*** Eliya anadziwa kuti nthawi yake yogwira ntchito ya Mulungu ili pafupi kutha, motero anachoka ku Phiri la Horebu kupita kukafuna Elisa, mnyamata amene adzapitiriza ntchito ya Mulungu. Eliya anapeza Elisa akulima m'munda *(onetsani zithunzi za mmene ankalimira mu nthawi ya Baibulo)*. Iye anavula chofunda chake ndi kufunditsa Elisa. Elisa anazindikira kuti ichi chinali chizindikiro chakuti wasankhidwa ndi Mulungu kuti asiye ntchito ya ulimi kuti akatumikire Mulungu. Iye anatsanzika abale ake ndipo anapita ndi Eliya kukayamba ntchito yatsopano. ***(1 Mafumu 19: 19-21)***<br>● Eliya ndi Elisa ankapita kulikonse limodzi pamene ankagwira ntchito ya Mulungu. *(Ngati nthawi ilipo, fotokozani za pa* ***2 Mafumu 2: 1-6****)*, ndi kutsindika kuti Elisa anatsimikiza zokhala ndi Eliya. Patapita nthawi pang'ono, anthu awiriwa anafika m'mbali mwa mtsinje wa Yordano. Fotokozani zomwe zinachitika pa ***vesi 8***. Eliya anatha kuchita izi chifukwa Mulungu anali naye ndipo anamupatsa mphamvu. Eliya anafunsa Elisa chomwe iye ankafuna asanatengedwe ndi Mulungu. Elisa anadziwa kuti iye adzafunanso mphamvu imene Mulungu amapereka yomwe inkathandiza Eliya kugwira ntchito ya Mulungu. *Fotokozani zokambirana za pa* ***2 Mafumu 2: 7-10.***<br>● Mwadzidzidzi chinthu chodabwitsa chinachitika akuyankhulana. Galeta ndi akavala amoto anaoneka pakati pa anthu awiriwa. Eliya ananyamulidwa kupita Kumwamba mu mphepo ya kamvuluvulu. Elisa sanathe kuonanso Eliya, koma chofunda chake chokha pansi. *Funsani ana za momwe Elisa ankamvera mu mtima (yekhayekha, kudabwa, chisoni).* ***(2 Mafumu 2: 11-12)***<br>● Elisa anatola chofunda chija ndi kubwerera ku mtsinje. Elisa ankaganiza ngati Mulungu anali ndi iye. *Fotokozani kuti Elisa anagwiritsa ntchito chofunda ndi zimene zinachitika* ***(vesi 14)*** Elisa tsopano anazindikira kuti Mulungu wa Eliya anali ndi iyenso ndi kuti adzamupatsa mphamvu zoti athe kugwira ntchito ya Mulungu. Mulungu adzamuthandiza monga momwe ankathandizira Eliya. ***(2 Mafumu 2: 13-15)***<br>● *Mulungu amagwiritsa ntchito anthu lero kuti agwire ntchito yake. Mwina ndi ntchito yokagwira m'dziko lina kapena m'dziko lanu lomwelo. Mulungu akufuna aliyense amene amakonda Iye kuti azigwira ntchito yake. Kodi tingatumikire Mulungu mu njira iti? Zina mwa zitsanzo zitha kukhala kukomera mtima ena, kuyitana ena kuti abwere ku tchalichi kapena kufotokozera ena za Yesu. Ife timatumikira Mulungu pokhala moyo umene umakondweretsa Iye. Chilichonse chimene mumachita kwa Iye, Mulungu adzakuthandizani – monga anathandizira Eliya ndi Elisa.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera – Elisa, mtumiki wa Mulungu watsopano / Elisa - Kuyitanidwa kutsatira. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***2 Mafumu 2: 14***. Tsindikani mawu a Elisa pofotokoza zomwe zinkachitika. |
| **KUMBUKIRANI** | Jambulani mizere yosonyeza kuti ndi galeta ndipo ana achekenire malawi a moto – penti, chekeni, pepala, kapena MAFUNSO:<br>● Kodi Eliya anakapeza ndani amene analowa m'malo mwake pa ntchito ya Mulungu?<br>● Kodi Elisa ankachita chiyani pamene Eliya ankamupeza?<br>● Kodi Elisa anachita chiyani?<br>● Kodi ndi ndani amene anagawa madzi mu mtsinje wa Yordano kuti anthu awiriwa awoloke?<br>● Kodi Elisa anapempha chiyani?<br>● Kodi chinabwera pakati pa Eliya ndi Elisa pamene Elisa ankatengedwa kupita Kumwamba ndi chiyani?<br>● Kodi Elisa anatola chiyani ndi kuchigwiritsa ntchito?<br>● Kodi tsopano Mulungu anali ndi Elisa? Elisa anadziwa bwanji?<br>● Kodi ndi ndani adzakuthandizani pa ntchito yanu ya Mulungu? |

## C10 Nkhani Yachiwiri

**Elisa – Kutonthoza bwenzi – Iyi ndi nkhani ya mphamvu ya Mulungu pa imfa.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Pemphero la Elisa linaukitsa mwana wa mayi.<br>● Ife titha kupemphera kwa Mulungu pamene takumana ndi zovuta pa miyoyo yathu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 4: 33***<br>**Ndime Yowerenga:** ***2 Mafumu 4: 8-37*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kodi munathandiza mnzanu wina? Kambiranani. Anthu akuthandiza abwenzi awo mu nkhaniyi. Kapena kodi mungayike chiyani mu chipinda chogona cha bwenzi lanu? Kodi iwo angafune chiyani? Mayi akumanga chipinda cha bwenzi lake mu nkhani yathuyi. |
| **PHUNZITSANI** | ● Elisa ankayendayenda m'dzikomo kugwira ntchito ya Mulungu. *Onaninso momwe Elisa analowera m'malo mwa Eliya komanso momwe Mulungu anamupatsira mphamvu zotumikira.* Iye nthawi zambiri ankapita ku Sunemu kumene kunali mayi wachuma ndi mwamuna wake. Iwo ankakonda kuyitana Elisa m'nyumba yawo kuti akadye. Ndipo patapita nthawi anaganiza zomanga chipinda chake pamwamba pa nyumba yawo kuti iye azigona usiku. *Fotokozani zomwe anayika mu chipindamo – bedi, mpando, tebulo ndi nyali. Banja limeneli linaoneketsa kukoma mtima kwa bwenzi lawo. Ifenso tikuyenera kuchita zimenezi kwa abwenzi athu.* ***(2 Mafumu 4: 8-10)***<br>● Elisa ankafuna kuwachitira kanthu kena pofuna kubwezera kukoma mtima kwawo. Iye anamva kuti mayi sankasangalala chifukwa analibe ana. Elisa anamuwuza kuti Mulungu adzamupatsa mwana wamwamuna! Pasanapite nthawi yayitali, mayiyo anabereka mwana wamwamuna. *Kodi mukuganiza kuti iye ankamva bwanji mu mtima mwake? (chisangalalo)* Zachisoni kuti tsiku lina mwanayo ali mnyamata ndipo akuthandiza abambo ake ku munda, anadwala kwambiri. Anamutenga kupita naye ku nyumba ndipo mosakhalitsa anamwalira. *Kodi mukuganiza kuti ndi ndani amene amayi ake anaganiza kuti akanawathandiza? (Elisa)* Mayiwa ankadziwa kuti Elisa anali munthu wa Mulungu ndipo akanatha kumuthandiza ndi mphamvu ya Mulungu. Iye anagoneka thupi la mwanayo pa bedi la Elisa, anakwera bulu wake ndi kupita ku nyumba ya Elisa. *Pamene muli pa mavuto kodi mumapita kwa yani kuti akakuthandizeni? (makolo, aphunzitsi, m'bale kapena mlongo)* ***(2 Mafumu 4: 11-25)***<br>● *Kwa ana a msinkhu uwu, zochitika izi tazilemba mosavuta.* Elisa anabwerera ndi mayiyo ndipo anapita mu chipinda chake kumene anagoneka thupi la mwanayo. Iye anatseka pa khomo ndi kupemphera kwa Mulungu. Iye anapumira mpweya mwa mnyamatayo ndipo mnyamatayo anakhalanso ndi moyo. Nthawi yomweyo anayetsemula ndi kutsekula maso ake. Mulungu anayankha pemphero la Elisa! Iye anapereka mwanayo kwa amayi ake. Mayi anali wokondwa kwambiri poona mwana wawo ali moyo! Elisa anakhulupirira Mulungu kuti amuthandiza ndi kuyankha pemphero lake. Mayiyo, mwamuna wake ndi mnyamatayo anaphunzira za mphamvu ya Mulungu tsiku limenelo. ***(2 Mafumu 4: 26-37)***<br>● *Chinthu chodabwitsa ichi chinachitika chifukwa Elisa anapemphera kwa Mulungu. Mulungu akufuna kuti tizimudalira ndi kupemphera kwa Iye pa nthawi yovuta pa moyo wathu. Kambiranani za zovuta zina – bwenzi lathu kuchoka, chiweto chathu kufa, wina wake kukuopsezani ku sukulu. Iye adzamvetsera mapemphero athu ndipo adzatithandiza. Mulungu adzasamalira amene amamukonda. Iye adzakhala nawo mu nthawi zawo zovuta.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa athandiza mayi wosauka / Elisa – Kutonthoza bwenzi. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***2 Mafumu 4: 33.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Ana ajambule zithunzi za zinthu zomwe angathe kupempherera kapena ayankhe mafunso:<br>● Kodi mayi wachuma ndi mwamuna wake anasamalira motani Elisa?<br>● Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa mayiyo?<br>● Kodi Mulungu anakwaniritsa motani lonjezo lake?<br>● Kodi mnyamatayo anali kuti pamene anayamba kudwala?<br>● Kodi amayi ake anagoneka pati thupi la mwanayo?<br>● Kodi iye anapita kwa ndani kukapempha thandizo?<br>● Kodi Elisa anachita chiyani pamene anafika ku nyumba ya mayiyo?<br>● Kodi Mulungu anayankha motani pemphero lake?<br>● Kodi tizichita chiyani pamene tili pa chisoni kapena ndi nkhawa? |

## C10 Nkhani Yachitatu

**Elisa – Kuchiritsa wakhate – Iyi ndi nkhani ya chikondi cha Mulungu pa munthu aliyense.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Namani anali ndi nthenda imene Mulungu yekha akanatha kuchiritsa.<br>● Mulungu anatipatsa njira yoti vuto lathu la tchimo likhululukidwe.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***2 Mafumu 5: 15***<br>**Ndime Yowerenga:** ***2 Mafumu 5: 1-19*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kodi mumapita kukaonana ndi ndani kuti akuchiritseni mukadwala? Kambiranani. Munthu wina mu nkhani yathu ankadwala ndipo panalibe amene akanatha kumuthandiza.<br>Kapena yankhulani za malangizo, olembedwa kapena oyankhulidwa. Munthu mu nkhani yathuyi ankayenera kumvera malangizo amene anapereka Elisa ngakhale kuti iye sankafuna kutero. |
| **PHUNZITSANI** | ● Namani, mkulu wa ankhondo a Mfumu ya Aramu, anali munthu wofunika kwambiri. Iye anali msilikali wolimba mtima, anapambana nkhondo zambiri ndipo mfumu inkakondwera naye kwambiri. Iye ankakhala m'nyumba yayikulu ndi mkazi wake ndi antchito ake. Koma anali mdani wa anthu a Mulungu, Aisrayeli. Tsiku lina chinthu choopsa kwambiri chinachitika. Iye atayang'ana khungu lake anaona kuti china chalakwika. Iye anali ndi khate – nthenda imene masiku amenewo adokotala sakanatha kuchiritsa. Posakhalitsa anthu ena adzaona kuti ali ndi nthenda imeneyi. Iye adzachotsedwa ntchito ndi kuchoka pakati pa abale ake. *Kambiranani zomwe anachita Namani atawuzidwa nkhani imeneyi.* ***(2 Mafumu 5: 1)***<br>● M'nyumba mwake munali mtsikana wantchito amene ankatumikira ndi kuthandiza mkazi wake. Iye anatengedwa ukapolo ku dziko la Israyeli ndipo anabwera m'nyumbamo monga kapolo. Iye anamva nkhani yoopsa ya Namani ndipo ankadziwa wina amene akanathandiza. *Kodi ndi ndani? (Fotokozani* ***vesi 3****)* Namani anavomera zopita kukaonana ndi Elisa. Khate linali vuto limene Namani sakanatha kulithetsa. *Ifenso tili ndi vuto limene sitingathe kulithetsa – tchimo limene limachititsa zoyipa.* Mfumu ya Aramu inalola Namani kuti apite akaonane ndi Elisa ndipo anamupatsa golide, siliva ndi zovala zoti akapereka kwa Elisa ngati mphatso. ***(2 Mafumu 5: 2-7)*** *Kodi Namani tsopano ankamva bwanji mu mtima mwake?*<br>● Namani atafika, Elisa anatumiza wantchito wake kuti akamuwuze kuti akasambe kasanu ndi kawiri mu mtsinje wa Yordano ndipo akachiritsidwa khate lake. Namani anapsa mtima kwambiri – iye anakwiya chifukwa Elisa sanatuluke kudzakumana naye ndiponso sankafuna kukasamba m'madzi a matope mu mtsinje wa Yordano. *Fotokozani momwe antchito a Namani anamulimbikitsa kuti atsatire malangizo a Elisa.* ***(vesi 13)*** *Ana a Kalasi 1 awerenge nthawi zimene Namani analowa m'madzi poyimirira, kuwerama, ndi kuweza manja awo.* Zodabwitsatu, Namani anachiritsidwa! Khungu lake linaoneka labwino kambiri. *Fotokozani zimene Namani ananena kwa Elisa.* ***(vesi 19)*** Namani tsopano anadziwa kuti Mulungu wa Israyeli ndi Mulungu woona. Namani anapereka golide, siliva ndi zovala monga mphatso, koma Elisa anakana kulandira. Anali Mulungu amene anachiritsa Namani, osati Elisa. ***(2 Kings 5: 8-19)***<br>● *Namani ankayenera kumvera zomwe Elisa ananena kuti achiritsidwe khate lake. Panalibe njira inanso yomwe iye akanachiritsidwira. Mulungu anayika njira kwa ife kuti vuto lathu la tchimo likhululukidwe. Tchimo limatilekanitsa ife ndi Mulungu. M'Baibulo, Mulungu akutiwuza kuti chifukwa cha Mwana wake, Yesu, amene anafa pa mtanda, titha kupempha Mulungu kuti atikhululukire tchimo lathu. Palibenso njira ina imene ife tingakhululukidwe tchimo lathu. Tikatero ife timalowa m'banja la Mulungu. Kodi munapempha Mulungu kuti akukhululukireni tchimo lanu? Iye adzatero ngati titamupempha.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Mulungu agwiritsa ntchito Elisa kuchiritsa munthu wodwala / Elisa – Kuchiritsa wakhate. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***2 Mafumu 5: 15***. Khazikika pa mawu anayankhula Namani – Mulungu wa Israyeli ndi Mulungu woona. |
| **KUMBUKIRANI** | Kalasi 1 – Uzani ana ajambule nkhope yachisoni yokhala ndi madontho mbali imodzi ndipo nkhope yosangalala yopanda madontho mbali ina ya pepala. Gwiritsani ntchito kuti afotokozenso nkhani.<br>● Kodi Namani ankagwira ntchito yotani?<br>● Kodi iye anali ndi nthenda yanji?<br>● Kodi ndi ndani anawuza Namani za Elisa?<br>● Kodi ndani analoleza kuti Namani apite akaonane ndi Elisa?<br>● Kodi Namani anabweretsa mphatso zotani?<br>● Kodi Namani ankayenera kukasamba kangati m'madzi mu mtsinje wa Yordano?<br>● Kodi Namani anachita chiyani atawuzidwa kuti akasambe mu mtsinje wa Yordano?<br>● Kodi ndi ndani amene anawuza Namani kuti amvere malangizo a Elisa?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani Namani atatuluka m'madzi nthawi yachisanu ndi chiwiri?<br>● Kodi iye anati chiyani kwa Elisa?<br>● N'chifukwa chiyani Elisa sankafuna kulandira mphatso?<br>● Kodi tili ndi vuto lotani lomwe ndi Mulungu yekha angalithetse? |

## C10 Nkhani Yachinayi

**Elisha – Chinyengo chilangidwa - Iyi ndi nkhani ya kunena zoona.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Mulungu analanga Gehazi chifukwa cha mtima wadyera ndi kunena mabodza.<br>● Yesu analangidwa chifukwa cha tchimo lathu pamene anafa pa mtanda.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Numeri 32: 23***<br>**Ndime Yowerenga:** ***2 Mafumu 5: 19-27*** |
| **MAWU OYAMBA** | Kambiranani za tanthauzo la kukhala wadyera. Kapena kodi ndi bwino kuyankhula bodza? Pamene tikuchita zinthu zimenezi, timaganiza kuti palibe wina amene adziwe kapena kuzindikira monga mmene zinachitikira mu nkhaniyi.<br>Onetsani zinthunzi kapena yankhani mafunso pofuna kubwereza nkhaniyi, kenaka zimene zinachitika ndi izi. |
| **PHUNZITSANI** | ● *(Fotokozaninso nkhani ya Namani, ngati simunayankhule poyamba phunziro.)* Namani, mkulu wa ankhondo, iye pamodzi ndi anthu ake ananyamuka kubwerera kwawo. Namani anali wosangalala chifukwa anachiritsidwa khate lake ndipo tsopano ankadziwa kuti Mulungu wa Elisa ndi Mulungu woona. Koma alipo wina amene sankasangalala. (Kodi iyeyu ndi ndani?) Gehazi, wantchito wa Elisa, anakwiya kwambiri chifukwa mbuye wake sanalandire mphatso zasiliva ndi zovala zabwino kuchokera kwa Namani. *Kodi mungakumbukire chifukwa chomwe Elisa sanalandire mphatsozo? Anali Mulungu amene anachiritsa Namani osati Elisa.* Gehazi anaganiza kuti kunali kopusa kwa Elisa kusalandira kanthu kuchokera kwa Namani ndipo anakonza zoti apite akatenge mphatso zina. Gehazi ankaonetsa dyera lake. Gehazi analakwitsa ponena bodza kuti apeze zomwe ankafuna. ***(2 Mafumu 5: 19-20)***<br>● Gehazi anathamangira Namani angakhale kuti anali atayenda mtundu wautali. Pamene Namani anaona Gehazi akuthamanga, iye anatsika pa kavalo wake ndipo anafunsa Gehazi ngati zonse zinali bwino. Fotokozani yankho la Gehazi pa ***vesi 22***. Gehazi anapereka nkhani imene sinali yoona ndi cholinga choti atenge siliva ndi zovala zabwino. Mulungu ananena kuti tisamanene zabodza. Onani pa ***Eksodo 20: 16***. Gehazi ananamiza Namani kuti amupatse mphatso zomwe zinali za Elisa. Namani anamupatsa Gehazi zambiri kuposa zomwe iye ankafuna! Iye anatumiza antchito ake awiri kuti athandize Gehazi kunyamula mphatso kupita nazo kwawo. *Ifenso taphwanya Malamulo a Mulungu ndipo nthawi zina timanena zabodza kuti tipulumuke ku mavuto kapena tipeze chinthu chomwe si chathu.* **(2 Mafumu 5: 21-23)**<br>● Antchito anamupatsa Gehazi mphatso ndipo anazibisa m'nyumba mwake. Iye ankaganiza kuti palibe amene akanadziwa zomwe wachita. *Kodi mukuganiza kuti ankalondola? Ndani anadziwa? Mulungu! Mulungu amadziwa pamene ife tachita zinthu zolakwa. Iye amadziwa chilichonse. Iye sakondwera pamene tikuchita chinyengo kapena kunama.* ***(2 Mafumu 5: 24)***<br>● Gehazi anapita kwa Elisa ndi kuyima pamaso pake. *Fotokozani zokambirana zawo mu **vesi 25-26**. Fotokozani kuti Mulungu anali atamuwuza Elisa zimene wantchito wake anachita.* Mulungu analanga Gehazi chifukwa cha choyipa chomwe anachita. Mulungu sanalole kuti iye akhale wosalangidwa. Mulungu anaona machimo ake. Nthawi yomweyo Gehazi anakhala wakhate. ***(2 Mafumu 5: 25-27)***<br>● *Baibulo limanena kuti tonse timachita zinthu zoyipa. Tonse tinachimwa. Mulungu amadziwa zonse zimene tachita. Ife titha kupempha Mulungu kuti atikhululukire machimo athu chifukwa cha Mwana wake Yesu, amene analangidwa chifukwa cha tchimo pamene anafa pa mtanda. Kodi inu munapempha Mulungu kuti akukhululukireni tchimo lanu?*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera B – Elisa ndi wantchito wake wadyera / Elisa – Chinyengo chilangidwa. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Numeri 32: 23***. Fotokozani kuti anthu ena amaganiza kuti palibe amene angadziwe tchimo lawo, koma Mulungu amadziwa chilichonse. Mulungu adzawadziwa machimo awo. |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● N'chifukwa chiyani Gehazi ankaganiza kuti mbuye wake anali wopusa?<br>● Kodi Gehazi anachita chiyani?<br>● Kodi iye ananena chiyani kwa Namani?<br>● Kodi mungafotokoza zotani za Gehazi?<br>● Kodi ndi ndani anathandiza Gehazi kunyamula mphatso za Namani kupita ku nyumba yake?<br>● Kodi Gehazi anaziyika kuti mphatsozo?<br>● Kodi iye ankaganiza kuti sadziwika zomwe wachita? Ndi ndani amene anadziwa?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani kwa Gehazi?<br>● Kodi ife tichite chiyani ndi tchimo lathu, zinthu zimene timalakwitsa? |

## <u>C11 Nkhani Yoyamba</u>

**Yona mu sitima ya pamadzi – Iyi ndi nkhani ya Mulungu kudziwa zonse za ife.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Yona sanamvere ndipo anayesa kubisala kuti Mulungu asamuone.<br>● Mulungu akufuna kuti ife tizimumvera.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yona 1: 3***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yona 1: 1-9*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani kwa ana za njira zosiyanasiyana za kuyankhulana wina ndi mnzake – kulemba, pa foni, kalata, ndi zina zambiri. Kambiranani momwe Mulungu amayankhulira kwa ife. Baibulo ndi Mawu a Mulungu. Pamene tikumvetsera kapena kuwerenga, Mzimu Woyera amabweretsa uthenga m'miyoyo yathu. Fotokozerani ana kuti mu Chipangano Chakale Mulungu ankatumiza mawu ake kudzera mwa anthu otchedwa aneneri. Anthu awa ankatumidwa ndi Mulungu ku malo osiyanasiyana kukapereka uthenga wa Mulungu kwa anthu amene ankakhala kumeneko. |
| **PHUNZITSANI** | ● Mulungu anayankhula ndi mneneri wotchedwa Yona ndi kumuwuza kuti apite ku Nineve. Unali ulendo wautali kuchokera kumene Yona ankakhala *(makilomita 800 – perekani chitsanzo cha kutalika kwake).* Anthu a kumeneko sankadziwa Mulungu ndipo ankakhala moyo wauchimo. Utumiki wa Yona unali oti akawawuze za chilango cha Mulungu ngati sasiya ndi kulapa *(kudzimvera chisoni). Fotokozani momwe Yona anamvera mu mtima mwake pamene anamuwuza kuti achite izi – mantha, kudzimvera chisoni ndi zina zambiri.* ***(Yona 1: 1-2)***<br>● Yona anaganiza zothawa ndi kupita dera lina kuti athawe pamaso pa Mulungu. *Kambiranani ngati ndi kotheka kuthawa pamaso pa Mulungu podziwa kuti Mulungu ali ponseponse ndipo nthawi zonse amationa.* Yona anapita ku Yopa kumene anakwera sitima ya pamadzi yopita ku Tariso. ***(Yona 1: 3)***<br>● *Fotokozani za namondwe owopsa amene Mulungu anatumiza - mkokomo wa mphepo ndi mafunde akuwomba sitima, zinthu kumagwa.* Oyenda sitima anali ndi mantha akulu ndipo anapemphera kwa milungu yawo. *Fotokozani kuti pakuti sankadziwa Mulungu woona, mapemphero awo sanayankhidwe.* Mothedwa nzeru anayesera kupeputsa sitimayo potaya katundu wina m'madzi. Nthawi yonseyi Yona anali atagona tulo m'sitimamo ndipo sankadziwa zonse zinkachitika. Mkulu wa oyendetsa sitimayo anamudzutsa ndi kumuwuza kuti apemphere kwa Mulungu wake kuti adzapulumutse sitimayo. ***(Yona 1: 4-6)***<br>● Oyendetsa sitima ankakhulupira kuti namondwe anabwera chifukwa cha kulakwa kwa munthu wina m'sitimamo. *Fotokozani m'mene ankachita maere pogwiritsa ntchito udzu kapena chinthu china.* Yona ndiye anasankhidwa! Iwo anafunsa Yona kuti anali ndani komanso kumene ankachokera. Yona anafotokoza kuti anali Mhebri amene ankatumikira Mulungu wa Kumwamba, amene analenga nyanja ndi mtunda ndi zilizonse zili m'menemo. Iye anawawuza kuti namondweyo anabwera chifukwa cha kulakwa kwake pakuti ankathawa pamaso pa Mulungu. ***(Yona 1: 9)***<br>● *Fotokozani kuti tikamawerenga Baibulo ndi kuphunzira zimene Mulungu amafuna kuti tizichita, ife tikuyenera kumvera uthenga wake osati kuchita zomwe anachita Yona.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yona mu sitima ya pamadzi. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yona 1: 3***. |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi Yona anali ndi ntchito yotani?<br>● Kodi Mulungu ankafuna kuti Yona apite kuti?<br>● N'chifukwa chiyani Yona sankafuna kupita kumeneko?<br>● Kodi Yona anayesera kuchita chiyani?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani sitima itayamba kuyenda?<br>● Kodi Yona ankachita chiyani nthawi ya namondwe?<br>● Kodi oyendetsa sitima anadziwa bwanji kuti chinali chifukwa cha Yona?<br>● Kodi Yona anati ankatumikira ndani? |

## C11 Nkhani Yachiwiri

**Yona pa nyanja – Iyi ndi nkhani ya momwe Mulungu amapulumutsira.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Mulungu anayankha pemphero la Yona ali m'mimba mwa chinsomba.<br>● Mulungu adzamva mapemphero athu pamene tifuwulira kwa Iye.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yona 2: 9***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yona 1: 10-17 ndi 2: 1-10*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani za nthawi imene zochita za ena zimabweretsa mavuto osati kwa iwo okha komanso kwa anzawo. Monga pa sukulu wina achita cholakwa chomwe chibweretsa chilango aliyense m'kalasimo, wina akuyendetsa galimoto moyipa, wina sakutsatira malangizo abwino a ukhondo. Kumbutsani ana za Yona kuti kusamvera kwake kunachititsa aliyense m'sitima akhale pa chiopsezo. |
| **PHUNZITSANI** | ● Oyendetsa atazindikira chimene Yona anali ndi amene ankamutumikira anachita mantha kwambiri. Iwo anafunsa Yona zoti achite kuti namondwe asiye kuwaononga. Yona anawawuza kuti chinali chifukwa chake pakuti ankathawa pamaso pa Mulungu, ndi kuti iwo ankayenera kumuponya m'madzi. Anthuwo sanafune kupha Yona, choncho anayesetsa kuti akafike ku mtunda koma namondwe anakula kwambiri. Kenaka oyendetsa sitima anafuwula kwa Mulungu ndi kumupempha kuti asawalange chifukwa cha kupha Yona. Iwo ananyamula Yona ndi kumuponya m'nyanja. Nthawi yomweyo namondwe anasiya ndipo nyanja inakhala bata. Anthu amene anali mu sitima anazindikira chomwe Mulungu anali ndipo anamutamanda ndi kumupembedza. ***(Yona 1: 10-15)***<br>● Pamene Yona ankamira, Mulungu anatumiza chinsomba chomwe chinamumeza. Thandizani ana kuti amvetse zomwe zinkamuchitikira Yona. ***(Yona 1: 17)***<br>● Yona anachita chinthu chokhacho chinali choyenera! Iye anapemphera kwa Mulungu. Yankhulani zakuti Mulungu amamva mapemphero posatengera kumene tili. M'pemphero lake Yona anayankhula zomwe Mulungu anali atamuchitira kale. Iye anakumbukira za kuti ankaganiza kuti akufa pamene ankamira pansi pa nyanja. Iye anakumbukira kuti analirira kwa Mulungu ndi kuti Mulungu anamva pemphero lake ndi kupulumutsa moyo wake. Iye anayamika Mulungu chifukwa cha kumva pempho lake. Iye anavomereza kuti Mulungu ndi Mulungu yekhayo woona, ndipo anati anthu amene amapemphera kwa mafano sangapulumutsidwe ndi milungu yawo. Yona anatamanda Mulungu pokhala Mulungu yekhayo amene amapulumutsa. ***(Yona 2: 1-9)***<br>● Atatha masiku atatu, usana ndi usiku, m'mimba mwa chinsomba, Mulungu analamula chinsomba kuti chilavule Yona pa mtunda powuma. ***(Yona 2: 10)***<br>● Mulungu analanga Yona chifukwa cha kusamvera kwake komanso anapereka njira yopulumukira (chinsomba) pamene iye analapa ndi kuvomereza tchimo lake. Ifenso tikuyenera kulangidwa chifukwa cha machimo athu, koma Mulungu anapanga njira yoti tikhululukidwe kudzera mu zimene Ambuye Yesu anachita. Monga Yona, ife tikuyenera kulapa tchimo lathu. Mulungu ndi wokonzeka kutipulumutsa ku tchimo lathu pamene tamupempha.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yona pa nyanja. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yona 2: 9***. |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana ayankhe mafunso ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi poyamba oyendetsa sitima anachita chiyani Yona atawawuza kuti amuponyere m'nyanja?<br>● N'chifukwa chiyani sankafuna kuponya Yona m'nyanja?<br>● Kodi chinachitika ndi chiyani ataponya Yona m'nyanja?<br>● Kodi oyendetsawo anachita chiyani ataona kuti namondwe wasiya?<br>● Kodi Mulungu anatumiza chiyani kuti chipulumutse Yona?<br>● Kodi Yona anakhala nthawi yotalika motani m'mimba mwa chinsomba?<br>● Kodi Yona anachita chiyani ali m'mimba mwa chinsomba?<br>● Kodi Yona anaphunzira chiyani?<br>● Kodi inu muli ngati Yona motani?<br>● Kodi Mulungu angathe kutipulumutsa motani? |

## C11 Nkhani Yachitatu

**Yona alalikira ku Nineve – Iyi ndi nkhani ya kutembenukira kwa Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Anthu a ku Nineve analapa ndi mtima wawo ndipo Mulungu anawakhululukira.<br>● Ife tikuyenera kulapa tchimo lathu kuti Mulungu atikhululukire.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Yona 3: 5***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yona 3: 1-10*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana za:<br>1) nthawi zimene anakakamizidwa kuti apepese ngakhale iwo sankafuna.<br>2) nthawi zimene ankadziwa kuti achita cholakwa ndipo ndi olakwa.<br>3) kuyankhula za kulakwa ndi mtendere umene amawupeza akavomereza kuti alakwitsa.<br>Kambiranani za kuonetsa khalide loti munthu walapa khalidwe lake loyipa. Lero tiona momwe anthu a ku Nineve anaonetsera kulapa kwawo. |
| **PHUNZITSANI** | ● Nthawi yomwe Yona atatuluka m'mimba mwa chinsomba Mulungu anayankhula nayenso, kumuwuza kuti apite ku Nineve akapereke uthenga wa Mulungu. Nthawi iyi Yona anamvera Mulungu nthawi yomweyo. Nineve unali mzinda waukulu kwambiri ndipo zinatenga masiku atatu kuti ayende kudutsa pakati pake. Yona anayamba kuwuza anthu kuti Mulungu adzawaononga chifukwa cha zoyipa zawo. ***(Yona 3: 1-4)***<br>● Mosayembekezeka anthu anakhulupirira uthenga wa Yona ndipo anadzimvera chisoni chifukwa cha zimene anachita. Iwo anafuna kuonetsa Mulungu za kulapa kwawo. Iwo anasala za kudya (osadya) ndi kuvala ziguduli m'malo mwa zovala zawo za nthawi zonse. Iyi inali njira yoonetsa kuti iwo anali osayenera ndipo kuti akulapa ndi mtima wawo wonse. ***(Yona 3: 5)***<br>● Pamene nkhaniyi inafika kwa mfumu, iyo inachoka pa mpando wake waufumu, inavula mkanjo wake ndi kuvala chiguduli. Iye analamula kuti aliyense mu mzindamo kuphatikiza ziweto zonse, asadye kanthu kalikonse ndipo avale ziguduli. Iye analamulanso kuti munthu aliyense asiye njira yake yoyipa ndi kupemphera kwa Mulungu. Mfumu inkayembekezera kuti Mulungu adzaona ndi kumva kulira kwa anthu ake ndipo adzasiya chikonzero chake chowaononga. ***(Yona 3: 6-9)***<br>● Mulungu anaona kuti anthuwa analapa ndi mtima wonse ndi kuti asiya tchimo lawo ndi kuti sakuchita chionetsero chabe kuti apulumutse miyoyo yawo. Iwo anakonzeka kusintha, kutembenuka kusiya njira zawo zoyipa ndi kutembenukira kwa Mulungu. Baibulo likugwiritsa ntchito mawu akuti **kutembenuka** pofuna kufotokoza zomwe anachita. Mulungu anasintha maganizo ake pa iwo powakhululukira ndi kusiya osawaononga.<br>● *Fotokozani kuti Mulungu lero ndi wachifundo ndi wokhululukira. Ngati anthu a ku Nineve, tikatembenukira kwa Mulungu, kulapa tchimo lathu ndi kukhulupirira uthenga wake, ifenso tidzapulumutsidwa.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yona m'mimba mwa chinsomba / Yona alalikira ku Nineve. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Yona 3: 5.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi Mulungu tsopano anafuna kuti Yona achite chiyani?<br>● Kodi zinatenga masiku angati kuyenda kudutsa mzinda wa Nineve?<br>● Kodi anthu anachita zinthu ziwiri ziti pofuna kusonyeza kuti alapadi?<br>● Kodi mfumu inachita chiyani kusonyeza kuti yalapadi?<br>● Kodi mfumu inalamula kuti anthu achite chiyani?<br>● Kodi Mulungu anaganiza zochita chiyani?<br>● Kodi tikuyenera kulapa chiyani?<br>● Kodi Mulungu adzatichitira chiyani ngati tilapa? |

## C11 Nkhani Yachinayi

**Yona apemphera kwa Mulungu – Iyi ndi nkhani ya chikondi ndi kukoma mtima kwa Mulungu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Nkhani ya Yona ikutionetsa chithunzi cha zimene Yesu anachita.<br>● Mulungu amakonda ndi kusamalira anthu onse.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Mateyu 12: 41***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Yona 4: 1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana momwe ndi pamene akuganiza kuti munthu wina wachitira zolakwa ndipo tikufuna kuti alangidwe. Nthawi zina timatha kuwuza makolo kapena aphunzitsi za munthu wina amene akuchita zolakwika ndipo timakhumudwa ngati tikuona kuti palibe chimene chikuchitika ndipo sakulangidwa moyenera. Umu ndi mmene Yona anamvera mu mtima ndi Mulungu mu nkhani ya lero. |
| **PHUNZITSANI** | ● Ngakhale Yona anamvera Mulungu kachiwiri popita ku Nineve, anakwiya kwambiri chifukwa Mulungu anakhululukira anthuwo. Iye ankadziwa kuti Mulungu ndi wachifundo, wochedwa kupsa mtima ndi wodzaza ndi chikondi, koma iye anakwiya chifukwa Mulungu anachita izi kwa anthu a ku Nineve. Yona analinso ndi zina zoti aphunzire! ***(Yona 4: 1 - 3)***<br>● Yona anatuluka mu mzinda ndi kukhala pansi kufuna kuona zomwe Mulungu achite. Linali tsiku lotentha kwambiri. *Funsani ana momwe amamva pamene kukutentha kwambiri ndi chimene chikhoza kuthandiza.* Mulungu anakwaniritsa chokhumba cha Yona pomeretsa chitsamba kuti chimuteteze ku kutentha kwa dzuwa. Usiku umenewo Yona anagona pansi pa chitsamba chimenechi. ***(Yona 4: 5 - 6)***<br>● M'mawa tsiku linalo, Mulungu anatumiza mbozi imene inadya chitsambacho. Chitsamba chinawuma mofulumira ndipo chinafa. Kenaka Mulungu anatumiza mphepo yotentha ndipo dzuwa linatentha Yona ngati poyamba paja. *Kodi tsopano akumva motani? Fotokozani kuti kwa nthawi yachiwiri, iye anapsa mtima ndi Mulungu koma tsopano chifukwa cha chitsamba.* Ndipo Mulungu anayankhula ndi Yona za kukhudzidwa kwake ndi chitsamba chimene iye sanachidzale ndipo chinalipo kwa kanthawi kochepa. Mulungu anafotokoza kuti Iye anali ndi udindo waukulu wochitira chisoni anthu a ku Nineve. Anthuwo analipo 120,000 *(fananizani ndi anthu ku dera lanu)* amene ankayenera kudziwa njira za Mulungu. N'chifukwa chake anawapatsa mwayi oti alape. Iwo anali ofunika pamaso pa Mulungu ndipo palibe anali oyipa kwambiri kuti sankayenera chikondi cha Mulungu! *Kambiranani kaganizidwe ka Yona za anthu a ku Nineve ndi chitsamba kuti kunali kudzikonda m'malo moti amvetsetse mtima wachikondi wa Mulungu pa anthu.* ***(Yona 4: 7 - 10)***<br>● *Mulungu amakonda ndi kusamalira anthu onse ngakhale atakhala kuti samvera njira zake. N'kofunika kuti aliyense pa dziko lapansi amve nkhani yabwino ya Ambuye Yesu.*<br>● Fotokozani kuti pamene Yesu anali pa dziko lapansi Iye anayankhula kwa anthu za Yona. Iye anawawuza kuti adzakhala m'manda masiku atatu masana ndi usiku, monga ngati nthawi imene Yona anakhala m'mimba mwa chinsomba. Iye anawawuzanso kuti anthu za Nineve adzapsa mtima ndi anthu amene anamva za Yesu koma osakhulupirira chifukwa iwo anamva uthenga wochokera kwa Yona, anamvetsera ndi kulapa. Yesu anali wamkulu kuposa Yona ndipo tikuyenera kumukhulupirira. ***(Mateyu 12: 40-41)***<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI Zoonjezera C – Yona mu mzinda / Yona apemphera kwa Mulungu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Mateyu 12: 41.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● N'chifukwa chiyani Yona anakwiya ndi Mulungu?<br>● Kodi Yona ankafuna kuti chimuchitikire chiyani?<br>● Kodi Yona anapita kuti?<br>● Kodi Mulungu anatumiza chiyani kudzathandiza Yona?<br>● Kodi chinachitika chiyani pa chitsamba?<br>● N'chifukwa chiyani Yona anakwiya?<br>● Kodi tikuphunzira chiyani za momwe Mulungu ankamvera mu mtima za anthu a ku Nineve?<br>● Kodi nkhani ya Yona ikufanana motani ndi zomwe zinachitikira Yesu? |

## C12 Nkhani Yoyamba

**Mulungu atumiza Mwana wake, Yesu – Iyi ndi nkhani ya kubadwa kwa Yesu.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Yesu, Mwana wa Mulungu, anabadwira ku Betelehemu.<br>● Yesu anabadwa kudzakhala Mpulumutsi wa dziko lapansi.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***1 Yohane 4: 14***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 1-7*** |
| **MAWU OYAMBA** | Onetsani ana zithunzi za ana akhanda. (Ngati n'kotheka onetsani chithunzi chanu muli khanda kapena ana abweretse zithunzi zawo ali makanda.) Kambiranani kumene ana amabadwira, malo monga chipatala, komanso chisamaliro chawo akabadwa, monga zovala zawo ndi pamene amawagoneka. Fotokozani kuti lero aphunzira nkhani ya khanda limene linabadwa pa malo osiyana ena. |
| **PHUNZITSANI** | ● Mfumu ya Chiroma inkafuna kudziwa kuti m'dziko mwake munali anthu ochuluka motani. Iye analamula kuti aliyense apite kumene anabadwira kuti akachite kalembera. ***(Luka 2: 1-3)***<br>● Yosefe ndi Mariya ankakhala ku Nazarete. Iwo anali pa ubwenzi woti adzakwatirana. Mariya anali pafupi kubwereka mwana. Kwa Yosefe ndi Mariya, ankayenera kuyenda ulendo kuchokera ku Nazarete kupita ku Betelehemu. ***(Luka 2: 4-5)*** *Fotokozani kutalika kwa ulendo umenewu (pafupifupi makilomita 130) ndipo kwa ana a Kalasi 2, gwiritsani ntchito mapu ngati alipo. Ana akambirane kumene mwina makolo awo akangapite ngati atapereka lamulo limeneli lero.*<br>● Iwo ali ku Betelehemu, mwana anabadwa. Mariya anakulunga mwana wake mu nsalu ndi kumugoneka modyera ng'ombe chifukwa m'nyumba ya alendo munalibe malo. *Fotokozani kuti anamugoneka m'mene ziweto zinkadyeramo ndipo kambiranani ngati malo amenewa anali abwino kwa mwana wakhanda (fotokozani zomwe zili mu m'Mawu Oyamba).* ***(Luka 2: 6-7)***<br>● *Fotokozani kuti ngakhale khanda limeneli, Mwana wa Mulungu, anali wapadera kwambiri pobadwa m'dziko lapansi, Iye anabadwa movutika kwambira ndipo anakulira m'banja la makolo osauka. Mulungu anaonetsa chikondi chake potumiza Mwana wake ku dziko lapansi ndipo tsiku lina mwana wakhanda ameneyu adzakula ndi kufa pa mtanda monga Mpulumutsi wa dziko lapansi. (Onani Vesi Yoloweza)*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mulungu atumiza Mwana wake, Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***1 Yohane 4: 14.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi ankalamulira dziko nthawi imeneyo anali ndani?<br>● Kodi mfumu inalamula kuti anthu onse achite chiyani?<br>● Kodi Yosefe ankafuna kukwatira ndani?<br>● Kodi Yosefe ndi Mariya ankakhala kuti?<br>● Kodi iwo ankayenera kupita kukachita kalembera kuti?<br>● Kodi chapadera chinali chotani ndi khanda limene linabadwa?<br>● Kodi Mariya anamukulunga mu chiyani?<br>● Kodi Mariya anagoneka khandalo malo otani? |

## C12 Nkhani Yachiwiri

**Mulungu atumiza Yesu, Mpulumutsi – Iyi ndi nkhani ya angelo kuonekera kwa abusa a ziweto.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Abusa a ziweto ndiye anali oyamba kuwuzidwa kuti Yesu wabadwa.<br>● Angelo analengeza chimene Yesu anali.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2: 11***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 8-15*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana za mayina. Afunseni ngati akudziwa chifukwa chimene anawapatsa dzina lawo kapena la mwana wakhanda m'banja mwawo. Yankhulani za banja, yankhulani zifukwa zimene anthu amapatsirana mayina. Funsani ana ngati anapatsidwa dzina lina osati limene akudziwika nalo monga losinjirira. Kumbutsani ana nkhani yam'mbuyo ya kubadwa kwa Mwana wa Mulungu. Uzani ana kuti khandalo analipatsa dzina lakuti Yesu komanso anapatsidwa mayina ena apadera kwambiri. |
| **PHUNZITSANI** | ● Kufupi ndi ku Betelehemu kunali abusa a ziweto kutchire kuyang'anira nkhosa zawo usiku. ***(Luka 2: 8)*** *Fotokozani kufunika koti abusa aziyang'anira nkhosa zawo usiku. Fotokozaninso kuti mwina ndi okhawo amene anali asanagone kuti amve nkhani yabwino imeneyi.*<br>● Mlengalenga munawala ndipo angelo anaonekera. *Funsani ana kuti aganizire momwe abusawo anamvera m'mitima mwawo (mantha, kudabwa, kudzidzimuka).* Mngelo anati kwa iwo "Musachite mantha. Ine ndakubweretserani Uthenga Wabwino wachimwemwe chachikulu umene udzakhala wa anthu onse. Lero m'mudzi wa Davide wakubwadwirani Mpulumutsi; Iye ndi Khristu Ambuye. Mwana wakhanda wakutidwa ndi nsalu atagona modyera ng'ombe." *Funsani ana kuti apeze mayina ena a Yesu monga Khristu, Ambuye ndi Mpulumutsi. Tsindikani pakuti Yesu anatchedwa Mpulumutsi chifukwa Iye adzapulumutsa dziko lapansi ku machimo awo. Fotokozani kwa ana kuti pamene Yesu anakula, Iye anafa pa mtanda kulangidwa chifukwa cha tchimo lathu kuti Iye akhale Mpulumutsi wathu. Fotokozani kuti "Khristu" zikutanthauza kuti Iye ndi wosankhidwa ndi Mulungu ndipo "Ambuye" zikutanthauza Iye ndi Bwana.* ***(Luka 2: 9-12)***<br>● Mwadzidzidzi, gulu lalikulu la angelo linaoneka mlengalenga likuyimba nyimbo zotamanda Mulungu kuti, "Ulemerero kwa Mulungu m'mwambamwamba, ndi mtendere kwa anthu pa dziko lapansi amene Iye akondwera nawo!" *Kumbutsani ana kuti Mulungu kutumiza Yesu ku dziko lapansi kudzakhala Mpulumutsi wathu chinali chinthu chopambana kwambiri ndipo monga angelo ankayamika Mulungu, ifenso tikuyenera kutamanda Mulungu ndi kumuyamika chifukwa cha chimene anatichitira.* ***(Luka 2: 13-14)***<br>● Pamene angelo anachoka, abusa a ziweto aja anayankhulana ndipo anati, "Tiyeni ku Betelehemu tikaone zinthu zomwe zachitika, zimene Ambuye atiwuza ife." ***(Luka 2: 15)***<br>● Thandizani ana kuti amvetse kuti Yesu anali mphatso yopambana kwambiri ya pa Khrisimasi imene Mulungu akanapereka kwa aliyense.<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Mulungu atumiza Yesu, Mpulumutsi. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 2: 11*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana ajambule chithunzi cha munda kumene kunali abusa a ziweto aja. Gwiritsani ntchito zinthu zosiyana – thonje, pepala lasiliva, kadi, nsalu, ulusi, penti ndi zina zambiri.<br>Kapena funsani ana ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi ndi ndani amene anali ku minda?<br>● N'chifukwa chiyani abusawa anali ku minda usiku?<br>● Kodi mlengalenga munaoneka chiyani?<br>● Kodi abusa anamva motani mu mtima mwawo?<br>● Kodi mngelo anati ndi ndani amene wabadwa?<br>● Kodi zinaoneka mlengalenga monse ndi chiyani?<br>● Kodi ankayimba nyimbo yanji?<br>● Kodi abusa anaganiza zochita chiyani? |

## C12 Nkhani Yachitatu

**Abusa a ziweto apeza Yesu – Iyi ndi nkhani ya alendo oyamba kudzaona Khanda.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Abusa anachitapo kanthu pa uthenga wa mngelo uja.<br>● Ifenso tikuyenera kuchitapo kanthu pa nkhani yabwino ya Yesu.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Luka 2: 20***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Luka 2: 16-20*** |
| **MAWU OYAMBA** | Yankhulani ndi ana za nthawi imene iwo anamva nkhani yabwino kwambiri. Perekani zitsanzo zanu, monga kumva za kubadwa kwa mwana kapena kumva kuti wina akubwera kudzakuchezerani. Afunseni kuti anamva bwanji mu mtima pamene anamva nkhani imeneyo ndiponso ngati anawuza wina za nkhaniyo. Kumbutsani nkhani yabwino imene abusa anayimva. (Nkhani Yachiwiri) |
| **PHUNZITSANI** | ● Abusa aziweto atamva nkhani yabwino ya Yesu, iwo sanachedwe kupita kuti akaone Khandalo. Iwo anafulumira ndipo anakapeza Mariya, Yosefe ndi khandalo. *Kodi iwo akanadziwa bwanji kuti afika ku malo olondola? (yankho—uthenga wa mngelo) Tsimikizani kuti Khandalo linali modyera ng'ombe monga ananenera mngelo.* ***(Luka 2: 16)***<br>● Iwo ataona Yesu, sanakhale chete ndi nkhani yabwinoyi. Iwo anafotokozera aliyense amene anakumana naye zomwe zachitika. Anthu amene anawawuza anadabwa kwambiri ndi zinthu zimene anamvazo. *Kumbutsani ana kuti kubadwa kwa Yesu ndi nkhani yopatsa chidwi mpaka lero. Lero, timadziwa nkhani inanso yopatsa chidwi ya kuti Iye anafa ndi kuuka. Monga abusa aja amene anafuna kufotokozera anthu onse amene ankakumana nawo za Yesu, ifenso titha kuwawuza anzathu za nkhani yabwino ya Yesu.* ***(Luka 2: 17-18)***<br>● Mariya anakumbukira zinthu zonse zimene zinachitika ndi kuzilingalira kwambiri. Abusa a ziweto anabwerera ku minda yawo koma sanayiwale zinthu zimene anazimva. Iwo anapitiriza kupereka ulemerero kwa Mulungu ndi kumutamanda chifukwa cha zinthu zazikulu zonse zimene iwo anaziona. ***(Luka 2: 19-20)***<br>● *Fotokozerani ana kuti pamene abusa anakumana ndi Yesu, miyoyo yawo inasinthika, ndipo sanayiwalenso zinthu zonse zimene zinachitika. Pamene tafika kwa Yesu ndipo Iye akhala Mpulumutsi wathu, miyoyo yathu imasinthikanso. Monga abusa aja anatamanda Mulungu, ifenso tikuyenera kuyamika Mulungu potipatsa Yesu kukhala Mpulumutsi wathu!*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Abusa a ziweto apeza Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Luka 2: 20.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa ngati njira yobwereza nkhaniyo:<br>● Kodi ndani anawuza abusa nkhani ya kubadwa kwa mwana watsopano?<br>● Kodi iwo anachita chiyani atamva nkhani yabwinoyi?<br>● Kodi abusawa anakapeza ndani atafika ku Betelehemu?<br>● Kodi khanda Yesu anali atagona motani?<br>● Kodi abusa anawuza ndani zinthu zimene iwo anaziona?<br>● Kodi ndani anakumbukira zinthu zimene zinachitika ndi kumalingalira?<br>● Kodi abusa anapita kuti atachoka ku Betelehemu?<br>● Kodi iwo anatamanda ndani? |

## C12 Nkhani Yachinayi

**Yohane abatiza Yesu – Iyi ndi nkhani ya kubatizidwa kwa Yesu mu Mtsinje wa Yordano.**

| | |
|---|---|
| | **Ife tikuphunzira kuti:**<br>● Yesu anabatizidwa ndi Yohane kuonetsa kuti anabwera kudzakhala ngati aliyense wa ife.<br>● Yesu ndi wosiyana ndi ife chifukwa Iye analibe tchimo.<br><br>**Vesi Yoloweza:** ***Marko 1: 7***<br>**Ndime Yowerenga:** ***Marko 1: 1-11*** |
| **MAWU OYAMBA** | Funsani ana ngati zinawachitikirapo kuti munthu wofunika kwambiri anabwera kudzacheza ku nyumba kwawo kapena ku sukulu kwawo kapenanso m'tawuni yawo. Ngati palibe, iwo aganizire za munthu wina wamkulu akubwera. Kambiranani za kukonzekera za munthu amene akubwerayo. Uzani ana kuti nkhani ya lero ndi munthu wina amene anakonza njira ya Yesu. |
| **PHUNZITSANI** | ● Yesu atabadwa, Baibulo silifotokoza zambiri za moyo wake mpaka pamene anali ndi zaka makumi atatu. Iye mwina anakulira ku Nazarete ndi abale ake ndi mwina ankagwira ntchito yopala matabwa monga Yosefe.<br>● Yesu anali ndi m'bale wake wotchedwa Yohane. Nthawi zambiri timadziwika kuti Yohane M'batizi. Yohane ankakhala mu chipululu kumene ankavala zovala za zikopa za gamila ndi kumadya dzombe ndi uchi wa kuthengo. ***(Marko 1: 6)*** *Fotokozani kuti izi zinali zachilendo.*<br>● Yohane M'batizi anakhala mlaliki. Udindo wake unali wokonzekeretsa anthu za kubwera kwa Khristu, Ambuye. Anthu ambiri ankapita kukamva uthenga umene Yohane ankalalikira. Anthu atalapa machimo awo (kutembenuka mtima), Yohane ankawabatiza (kutanthauza kuwamiza m'madzi). *Fotokozani kuti sanali madzi amene ankayeretsa tchimo lawo, koma chinali chizindikiro cha zomwe zachitika m'miyoyo yawo.* Iye anawawuza kuti munthu wina womuposa iye akubwera. Pamene iye anayankhula za Yesu, anati, "Ine si woyenera kumasula zingwe za nsapato zake." *Fotokozani kuti ndi kapolo amene ankagwira ntchito imeneyi kwa mbuye wake. Yesu anali wamkulu kwambiri kuposa Yohane ndipo Yohane anadziona kuti sanali woyenera kukhala kapolo wa Yesu.* Iye ananenso kuti tsiku lina Yesu adzabweretsa Mzimu Woyera pa anthu. ***(Marko 1: 4-5, 7-8)***<br>● Yesu ali ndi zaka makumi atatu, nthawi inakwana yoti Iye ayambe kuyitanira anthu kwa Mulungu ndi kulalikira nkhani yabwino yome angelo aja anayankhula tsiku limene Iye anabadwa. Yesu anapita ku mtsinje wa Yordano kumene Yohane ankalalikira ndi kubatiza anthu. Yohane anabatiza Yesu mu mtsinje wa Yordano. ***(Marko 1: 9)***<br>● *Fotokozerani ana kuti Yesu sankayenera kubatizidwa chifukwa analibe tchimo. Yesu anali Mwana wa Mulungu, motero Iye anali wangwiro ndipo sanachite choyipa chilichonse. Pamene Yesu ankabatizidwa, Iye ankadzifanizira ndi anthu ochimwa monga ife. Yesu anakhala ngati ife kupatula kuti analibe tchimo, ndi cholinga chakuti tsiku lina Iye adzapite pa mtanda ndi kufa kuti machimo athu akhululukidwe.*<br><br>**Tsirizani phunziro la Nthawiyabaibulo.**<br>**Onetsani:** Onani FBI pa Zoonjezera C – Yohane abatiza Yesu. |
| **PHUNZIRANI** | Phunzitsani ndi kufotokoza ngati n'koyenera Vesi Yoloweza: ***Marko 1: 7.*** |
| **KUMBUKIRANI** | Uzani ana kuti ayankhe mafunso awa kuti ikhale njira yobwereza nkhani:<br>● Kodi Yesu anakulira kuti?<br>● Kodi m'bale wake wa Yesu ankatchedwa ndani?<br>● Kodi Yohane ankadya chiyani ku chipululu?<br>● Kodi Yohane M'batizi anati ndi ndani amene ankabwera?<br>● Yohane M'batizi anati Yesu anali ____ kuposa iye. (lembani mawu amene palibe)<br>● Kodi Yesu anali ndi zaka zingati pamene anapita kwa Yohane?<br>● Kodi Yohane anachita chiyani kwa Yesu?<br>● N'chifukwa chiyani sankafunika kuti akhululukidwe machimo ake? |

# Malangizo a Aphunzitsi a Kachongedwe ka Maphunziro

**Maphunziro a Kalasi Yoyamba**
- Sabata lililonse pali masamba anayi amene akufunika kuchekenira ndi kulembamo mawu pang'ono.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 amene akuyenera kuperekedwa kuchokera pa marikisi 80 a mwezi onse.
- Ana amene akuphunzira maphunziro a Kalasi Yoyamba iwo sakuyenera kuwerenga chifukwa sangathe kuwerenga bwino ndipo tikuyembekezera makolo/owang'anira/atsogoleri awo kuwathandiza.

**Maphunziro a Kalasi Yachiwiri**
- M'buku muli maphunziro anayi pa sabata.
- M'phunziro lililonse muli nkhani. Ophunzira akuyenera kupeza mawu osiyanasiyana m'phunziro, ndi kuchekenira, kutsiriza Mavesi Oloweza ndi zina zambiri.
- Sabata lililonse pali marikisi 20 pa marikisi 80 a mwezi uliwonse pamene atsiriza maphunziro onse molondola.

**FUNDO ZA KACHONGEDWE**

Choyamba aphunzitsi akupemphedwa kuti:
- Onani phunziro lililonse ndipo chongani moyenera zolondola kapena zolakwitsa.
- Perekani marikisi amene mwalangizidwa kutero.
- Nthawi zonse chongani pogwiritsa ntchito mitundu yosiyana ya zolembera, CHONGANI yankho lolondola.
- Lembani yankho lolondola poyenera kutero ndi kukonza mawu olakwika kalembedwe ake, koma MUSACHOTSE marikisi.
- Perekani marikisi ochepa pa yankho lolondola mbali imodzi yokha.
- Phatikizani marikisi onse a pa mwezi ndipo lembani kumapeto pa malo amene mwapatsidwa.

N'kofunika kusaumira ndi kuchita chilichonse chothandiza kulimbikitsa ophunzira kuti aphunzire Baibulo lawo. N'zothandizanso kuti kumapeto kwa mwezi uliwonse mphunzitsi azilemba mawu a chilimbikitso kwa wophunzira pa malo amene aperekedwa. Mutha kulemba ndemanga yoyamikira kuchekenira bwino, zilembo zabwino ndi kumvetsa bwino phunziro ndi zina zambiri.

Yesetsani kuti ndemanga, mafunso, ziganizo, zomwe mwaona ndi zina zambiri zikhale zosiyanasiyana, kuti zithandize kupanga zinthu kukhala zosiyana. Izi zimafunika kuganiza bwino, ndipo ndi kofunika kuti wophunzira azikhala ndi chidwi nthawi zonse. Ngati chiganizo chomwecho kapena funso lomwe likubwera mwezi uliwonse, zimachotsa chidwi cha wophunzira.

**Kalasi Yoyamba**
**Ndemanga zina**
"Chikondi – Ine ndasangalala kuti inu mwayamba maphunziro awa ndipo ndikukhulupirira kuti muwakonda. Zochekenira zanu ndazikonda. Kodi mumapita ku sukulu? Ndikuyembekezera kumva kuchokera kwa inu posachedwa."
"Wachita bwino, Andreya. Wachekenira bwino kwambiri! Kodi zimavuta pamene mumachekenira mizere ya m'kati? Inu musiyako zochepa zokha munachekenira pang'ono phunziro lapita lija."

**Ndemanga zauzimu**
"Wachita bwino, Sarah. Yairo analitu munthu wokondwa kwambiri pamene Yesu anamuthandiza."
"Yankho labwino kwambiri! Nkhani ya kufa kwa Yesu ndi yomvetsa chisoni, koma chokondweretsa ndi chakuti Iye anaukanso."

**Kalasi Yachiwiri**
**Ndemanga zina**
"Yankho labwino, Chimwemwe – Ine ndikukhulupirira kuti aphunzitsi ako akusangalala kwambiri ndi ntchito yako ku sukulu!"
"Ine ndikudziwa kuti posachedwapa ndi tsiku lako lobadwa, Chisomo. Kodi udzachita phwando? Udzachitira kuti? Udzakhale ndi tsiku lopambana kwambiri!"
"Iwe wayesetsa kwambiri. Pali zolakwika zochepa chabe. Usamayiwale kuonanso mayankho nthawi iliyonse."

**Ndemanga zauzimu**
"Ine ndasangalala ndi mmene wachekenira chithunzi cha Yesu ali nkhanda modyera ng'ombe. Kodi sizinali zabwino kuti Mulungu atumize Mwana wake ku dziko lapansi kwa ife?"
"Mitundu yako ndayikonda kwambiri! Zakariya anapereka dipo chifukwa cha kusakhulupirira zimene Mulungu ananena. Iye anakayikiranso Mawu a Mulungu."
"Mayankho abwino kwambiri. Munthu amene anakumana ndi Filipo ku chipululu anapita kwawo akusangalala kwambiri. Iye anamva ndi kukhulupirira nkhani yabwino ya Yesu."

## Zoonjezera A - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C7 | Davide | **Davide ndi Jonatani / Davide akuthawa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-david-saul/ |
| | | **Davide mfumu/ Davide amusiya Sauli wosamupha** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-david-cave/ |
| | | **Davide atamanda Mulungu / Davide akhala mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/fn-david-mephibosheth/ |
| | | **Davide ndi Mefiboseti** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ls-mephibosheth/ |
| | | |
| C8 | Yoswa | **Yoswa akhala mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joshua-commander/ |
| | | **Yoswa ndi dziko latsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-rahab-spies/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joshua-commander/ |
| | | **Yoswa ndi Mtsinje wa Yordano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-joshua-jordan/ |
| | | **Yoswa ndi Yeriko** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joshua-commander/ |

## Zoonjezera A - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C7 | Davide | **Davide akuthawa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-jonathan/ |
| | | **Davide amusiya Sauli wosamupha** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-saul-cave/ |
| | | **Davide akhala mfumu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/saul-last-days/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/david-ark/ |
| | | **Davide ndi Mefiboseti** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-daniel/ |
| | | |
| C8 | Yoswa | **Yoswa akhala mtsogoleri watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/moses-joshua/ |
| | | **Yoswa ndi dziko latsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-joshua-commander/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-rahab-spies/ |
| | | **Yoswa ndi Mtsinje wa Yordano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jordan/ |
| | | **Yoswa ndi Yeriko** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/joshua-jericho/ |

## Zoonjezera B - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C9 | Eliya | **Eliya amvera Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-elijah-food/ |
| | | **Eliya adalira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-elijah-food/ |
| | | **Eliya apemphera kwa Mulungu / Eliya atumikira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-prophet-elijah/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elijah-baal/ |
| | | **Eliya apempheranso / Eliya ayiwala Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elijah-baal/ |
| | | |
| C10 | Elisha | **Elisa, mtumiki wa Mulungu watsopano** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elijah-elisha/ |
| | | **Elisa athandiza mayi wosauka** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elisha-oil/ |
| | | **Mulungu agwiritsa ntchito Elisa kuchiritsa munthu wodwala** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elisha-naaman-1/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elisha-naaman-2/ |
| | | **Elisa ndi wantchito wake wadyera** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/rg-elisha-naaman-2/ |

## Zoonjezera B - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| C9 | Eliya | **Eliya amvera Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-elijah-food/ |
| | | **Eliya adalira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/sb-elijah-food/ |
| | | **Eliya atumikira Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-prophet-elijah/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-prophets-baal/ |
| | | **Eliya akhumudwitsa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/photos/elijah-horeb/ |
| | | |
| C10 | Elisha | **Elisa - Kuyitanidwa kutsatira** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-elisha/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elijah-chariot/ |
| | | **Elisa - Kutonthoza bwenzi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-boy/ |
| | | **Elisa - Kuchiritsa wakhate** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-naaman/ |
| | | **Elisa - Chinyengo chilangidwa** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/elisha-naaman/ |

## Zoonjezera C - Kalasi 0 ndi Yoyamba Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| **C11** | **Yona** | **Yona mu sitima ya pamadzi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-preschool/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-jonah/ |
| | | **Yona pa nyanja** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-preschool/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-jonah/ |
| | | **Yona m'mimba mwa chinsomba / Yona alalikira ku Nineve** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-jonah/ |
| | | **Yona mu mzinda / Yona apemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-jonah/ |
| | | |
| **C12** | **Nkhani ya Khrisimasi** | **Mulungu atumiza Mwana wake, Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/birth-jesus-preschool/ |
| | | **Mulungu atumiza Yesu, Mpulumutsi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-christmas-story/ |
| | | **Abusa a ziweto apeza Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/yo-christmas-story/ |
| | | **Yohane abatiza Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/preschool-jesus-baptised/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-john-baptist/ |

## Zoonjezera C - Kalasi Yachiwiri Zithunzi Zaulere m'Baibulo

| | Mutu | Nkhani m'Chithunzi |
|---|---|---|
| **C11** | **Yona** | **Yona mu sitima ya pamadzi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-jonah/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-jonah/ |
| | | **Yona pa nyanja** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-jonah/ |
| | | **Yona alalikira ku Nineve** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-jonah/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-jonah/ |
| | | **Yona apemphera kwa Mulungu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/mk-jonah/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/jonah-disobeys/ |
| | | |
| **C12** | **Nkhani ya Khrisimasi** | **Mulungu atumiza Mwana wake, Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/ed-jesus-birth/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/bpa-christmas/ |
| | | **Mulungu atumiza Yesu, Mpulumutsi** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-shepherds/ |
| | | **Abusa a ziweto apeza Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/christmas-shepherds/ |
| | | **Yohane abatiza Yesu** |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/lgr-john-baptist/ |
| | | https://www.freebibleimages.org/illustrations/wdv-john-baptist/ |

© Bible Educational Services 2023

www.besweb.com

Registered Charity UK CIO 1186004

NY - 08/2025
(Chichewa)